


MBAMBANDE

 Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano kwa pemphero. Pamene mitu yathu ndi mitima yaweramira pamaso pa Mulungu, ine—ine ndikudabwa ndi angati muno ali ndi chopempha chimene iwo akufuna kuti Mulungu awakumbukire, pakungokweza manja anu? Tsopano, sungani chopempha chanu mu mtima mwanu tsopano pamene ife tikupemphera.

² Ambuye Yesu, Inu ka—Kasupe, Kasupe wosatha wa Moyo, yendererani kupyolera mwa ife lero, Ambuye, ndi kutiyeretsa ife ku kusakhulupirira konse ndi tchimo lonse, kuti ife tikhoze kuyima mu Kukhalapo Kwanu tsopano, podziwa kuti pali kusowa pakati pathu, kuti ife tikudziwa kuti ndife ochimwa ndi osati—osayenera za dalitso lirilonse. Koma ndiye pamene ife tilingalira za Iye Yemwe anadza natenga machimo athu! Ndiye, pamene Mwazi Wake uli pamenepo, sitiri—sitiri ife mu Kukhalapo kwa Mulungu, ndi Iye. Ndi liwu lathu chabe kupyolera mu Mwazi Wake. Mwazi Wake ukulankhula. O Mulungu, ndiye yeretsani mitima yathu kwa tchimo ndi kusakhulupirira.

³ Perekani kwa ife zokhumba za mtima wathu, pakuti ife moona tiri nazo zokhumba izi kuti tikutumikireni Inu. Mu zikhalidwe zooketsa izi, ndi zosautsa, ndi zinthu za mdziko zimene zimayikidwa pa ife nthawizina, kuti zitikhalitse ife angwiwo; ife tawuzidwa zimenezo. Ndiye Iye anati, “Musaganize icho nchachilendo kuti mayesero awa akudza.” Iwo akugwira kokha ntchito kwa ubwino wathu ndi kuti atikhalitse ife angwiwo, ndi kutibweretsa ife mu malo awo. Zipululu zazikulu izi za zotichitikira, kumene anthu olungama akuwumbidwa kukhala ojera, ife—ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha zotichitikira izi, Ambuye. Ife sitikanatanthauza, sichiri chanzeru kufuna kuchita chirichonse chotsutsana kwa chifuniro Chanu. Koma ife tikupemphera, Atate, kuti mu ichi ife tidzabweretsedwe pafupi kwa Inu.

⁴ Ndipo pamene akatundu ali olemera kwambiri ife sitingakhoze kupita patsogolo, ndiye ife tikukweza manja athu ndi kufuulira kwa Atate athu. Ndiye imvani kuchokera Kumwamba, Ambuye.

Tichizeni ife, tipangeni ife abwino, chifukwa cha Ufumu wa Mulungu.

Dalitsani Mawu Anu m'mawa uno, Ambuye. Mawu Anu ali Chowonadi.

⁵ Ndipo ife tasonkhana pano tsopano mu mpingo. Ife tikupempherera M'bale Neville, ndi M'bale Capps, ndi M'bale Collins, ndi atumiki ena onse, ndi—ndi matrasitii, madikoni,

ndi mamembala onse, ndi alendo mu zipata zathu. Mulole ili likhale tsiku limene ife tidzalikumbukire motalika, chifukwa cha Kukhalapo Kwanu.

⁶ Ife tiri pano pansu pa kuyembekezera kwakukulu mmawa uno, Ambuye. Kungodziwitsidwa mwakanthawi, kuitanidwa palimodzi. Ife tikumverera kuti ziri kwa cholinga. Mulole cholinga Chanu chikwaniritsidwe, Ambuye. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, pamene ife tikudzipereka tokha. Amen.

⁷ Chiri chopambana kukhala pano ndi kusonkhana ndi mpingo uno wodzaza anthu. Ine sindinali kuyembekezera kukhala nkomwe aliyense muno m'mawa uno, chifukwa ine sindinadziwe nkomwe, inemwini, kuti ine ndikhala pano.

⁸ Ife tangofika kumene kuchokera ku Philadelphia. Ndipo kotero ine ndinabwera mkati, ndikuganiza kuti ndimasowa kupita ku Arizona mwamsanga ndithu, kukakhala ndi ulaliki pa maliro a bwenzi la ine, Captain Jim Mosely, wofunika kwambiri, mnyamata waumulungu yemwe ine ndinamutsogolera kwa Khristu osati kale litali, a Mosely atatu apachibale. Ndipo m'modzi wa iwo anagwa, ndipo anali mu ndege tsiku lina, ndipo anaphedwa nthawi yomweyo. Anagona mu moto kwa maora khumi iwo asanafike kwa iye. Kotero Lee ali zaka makumi awiri zisanu ndi zitatu zakubadwa, mkazi wake makumi awiri zisanu ndi chimodzi, ndi—ndipo wasiya ana aang'ono atatu; wamkulu, zisanu ndi ziwiri. Zachisoni zedi. Ndipo iwo... Pamene iwo anadza naye iye mkati, ndiye iwo anali woti amuyike iye tsiku lotsatiralo. Kotero ine basi... Ine sindinapite nkomwe. Ndipo ine ndinangolembe, kapena kutumiza pa telegramu, zomwe ine ndinati ndikalankhule, kapena zomwe ndikanazilankhula pa maliro a M'bale Mosely. Zina mwa zinthu izi ife sitingakhoze kuzimvetisa, komabe Iye amapangitsa chirichonse kuchitika mwabwino basi.

⁹ Ife tiri muno mu msonkhano wa Ambuye, mmawa uno, podziwa kuti—kuti—kuti ife tikukhulupirira Mulungu, kuti ife tikukhulupirira kuti Iye adzapanga chirichonse chimodzimoto basi molondola. Mosasamala za chimene icho chiri, ndi momwe icho chimachitikira, ife tikudziwa izo ziyenera “kuchitika kwa ubwino.” Iye analonjeza izo. Ichu chiyenera kungokhala mwanjira imeneyo. Nthawizina ife sitingakhoze kumvetisa izo, zimakhala zosokonezeka kwambiri nthawi zina, komabe ife tikudziwa kuti ndicho choonadi, chifukwa Baibulo limati ndicho Choonadi. Ndipo Baibulo, kwa ife, liri Mulungu mmaonekedwe a kalata.

¹⁰ Tsopano, ife tiyenera kukhazika chikhulupiro chathu penapake. Ndipo ngati—ngati ine kapena wina wa ife, m'moyo, ayesa kuchita bwino m'moyo ndipo nkukhala, nthawi zambiri, wamamilioni ambiri, koma ife tichita nazo chiani zimenezo? Ife

tiyenera kubwera pansi pa mapeto a mseu, ndipo chiyani—ndi chaubwino wanj kwa ife ndiye? Mukuwona? Ndipo ndalama ndi—cholemba, ndi chosinthanitsa, koma inu simungakhoze kusinthanitsira iyo kuti upeze Moyo. Mulungu yekha ali nawo Moyo.

¹¹ Kotero ife—ife tikuzindikira kuti ife tiri pano mu maonekedwe a mthunzi. Ndipo ngati pali mthunzi, apo payenera kukhala chenicheni. Sipangakhale mthunzi popanda chenicheni, mukuwona, chifukwa ndi chifukwa cha chenichenicho chomwe chimapangitsa mthunziwo. Monga inu mukanakhala nawo mthunzi wa chithunzi wa chinthu china. Payenera kukhala chinthu penapake, kapena kukakhudza, kuwala kunakhudza galasi limenelo, kapena sipakanakhalanso wina—mthunzi wina. Kotero pamene ife powona kuti moyo wathu pano uli mu mthunzi, ndi podziwa kuti ife tiri mu chifaniziro cha moyo wina kwinakwake, ndiye ife tikudziwa kuti pali chenicheni kwinakwake chimene kuwala kwakhudza, ndipo icho chanyezimiritsa chinachake apa pa dziko lapansi. Ndipo ife tiri chabe chinyezimiritsa chimenecho. Chinthu chenichenicho chiri kwinakwake. Ngati izo siziri, ine ndine munthu wonyengedwa koposa m'dziko; ine ndataya moyo wanga pachabe. Koma ine ndikudziwa, mopanda mthunzi wa kukayika, kuti chiri kumeneko. Mukuwona? Ndicho chifukwa chake ife tiri pano. Mukuwona?

¹² Pamene ine ndikuwona inu anthu mukubwera kudutsa ndziko lonse, pa chidziwitso cha mphindi-zochepa, ndipo nthawizina kumapenekera, ndiye izo zimandipanga ine kuwoneka wochepa kwenikweni pamene ine ndibwera mu msonkhano wonga uwu; poganiza kuti ine ndikudziwa anthu pano ayenda kwa mitunda mazana, kudzangokhala muno kwa maminiti ochepa a utumiki, kudzangokhala muno.

¹³ Mkazi wina anachitirapo chabe ndemanga, anabwera mkati tsiku lina ndipo anati, “Mundiwonetse ine pamene mwamunayo wayendapo, ndipo mudirole ine ndiyende pambuyo pake, pa nthaka,” anati, “Ine ndikhala bwino.” Tsopano, anthu amakukhulupirirani inu motero, ndipo ndinu oyimira a Khristu, ndiye nanga ife tizichita chiyani? Ife tiyenera kukhala osamalitsa kwambiri, chifukwa inu simukungodziwononga nokha ndi cholakwika, inu mukuwononga enanso omwe akukutsatani inu.

¹⁴ Kotero, ine sindikudziwa chipembedzo kapena china choti ndingakutengereniko inu. Pali chinthu chimodzi chokha chomwe ine ndayikamo chikhulupiriro changa. Ngati inu mukundikhulupirira ine, tsatani zimene ine ndikukuuzani inu. Chifukwa, ine ndimakhulupirira Baibulo, ndiwo Mawu a Mulungu. Zinthu zina zimalephera. Ine ndiri chabe. . . Iye ali Moyo. Iye ali Mawu.

¹⁵ Tsopano, ine ndikudziwa kuti inu . . . Pamene ine ndibwera kuno, ine ndimakusungani inu motalika. Ine ndinapemphera kwa Mulungu, pamene ine ndinamverera ngati ine ndima funa kubwera kuno lero. Ine ndakhala nazo zolankhulana zapadera zambiri ndi kuyitana, ndi zina zotero! Ine ndinayenera kukomana nawo ena a iwo m'mawa uno. Ndipo ine ndinati, "Chabwino, M'bale Neville mosakayika andifunsa ine kuti ndilankhule." Ilo linali Lachisanu. Ndipo ine ndinati, "M'bale Neville mwina andifunsa ine kuti ndilankhule. Ndipo pamene ine nditero, ndiye ine ndikupemphera, Mulungu . . ." Ndi kotentha zedi, kwakhala kotentha kwambiri. Ndipo Iye anachita bwino kutitumizira ife mvula ndi kuchotsa kutentha kopitirira kwenikweni, ndi kutipatsa ife m'mawa wabwino m'mawa uno. Ine ndikupemphera kuti ubwino Wake uvumbire mmodzi aliyense wa inu nonse, kuti inu mudzakhale mukukumbukira kuti munalu muno mmawa uno. Chisomo Chake ndi madalitso zikhale pa inu!

¹⁶ Usiku wapitawu ine ndinakamuhezetsa mzanga yemwe akudwala, M'bale Bill Dauch. Ine sindikumuwona iye muno m'mawa uno. Mwinamwake, ine sichoncho. O, apa iye ali. Iye ali . . . Eya. Ndipo ine ndinali kuganiza, "Mwamuna wachikulire wa zaka makumi asanu ndi anayi ndi chimodzi zakubadwa, ndipo akukukumabe kupyola m—mdziko, kupyola zipululu, ndipo kudutsa mapiri achisanu ndipo misewu yoterera. Iye sayenera kuchita zimenezo. Mulungu wakhala wabwino kwa iye; iye sayenera kuchita zimenezo. Iye akanakhoza kukhala kunyumba nakhala nawo antchito akumukupizira iye, ngati iye akanafuna kutero." Koma, chinachake chinachitika kwa Bill Dauch, iye anabadwanso kachiwiri. Ndipo pamene izo zinatero, chinachake chinadza mu mtima wake, kuti chonse chomwe iye amakhallira moyo ndicho kukhala nawo pa misonkhano imeneyi. Ndiyeno ngati ine ndingakhale cholankhuliramo cha Mulungu, kodi ine ndinganyenge bwenzi? Kuli bwino ine ndife. Ndiye ndiroleni ine ndimuwuze iye chimodzimodzi chomwe chiri Choonadi kuchokera m'Baibulo ili. Ndiye, ndiwo Mawu a Mulungu. Ine ndikungobwereza chimene Iye ananena.

Tsopano ine ndikufuna kuwerenga zina zochokera m'Baibulo.

¹⁷ Ife tisanawerenge, ine ndikanakonda ku—kunena kuti ine ndikukhulupirira usiku uno ndi usiku wa mgonero. Ndipo inu amene mukukhala chakuno . . . Chifukwa, anthu ena mwina akhala akubwerera kunyumba zawo, chifukwa iwo ayenera kukapita ku ntchito. Inu amene muli akonkuno mu kusunkhana, kumbukirani, abale akhala akupereka mgonero usiku uno.

¹⁸ Tsopano, ine ndikuyembekezera ku—kuyitana komaliza kwa ku Afrika. Iwo samafuna, sangandilore ine kukalowa monga mmishonare. Kotero njira yokha ine ndikhoza kuloweramo, kumusi . . . Ine ndikupita ku Kenya, Uganda, ndi—

ndi Tanganyika. Ndipo njira yokha imene ine ndingakhoze kupitiramo... Choyamba, mipingo siyingakulole iwe kulowamo, chifukwa iwo akufuna ine kuti ndizilalikira chinachake cha mbali *iyi* ndi mbali *iyi*, kumusi mu Afrika. Ndipo ine sindikanadzapita monga choncho. Ine sindingakhale wonyenga mokwanira kukachita izo. Kotero ine mwina ndiwauza iwo, “Ayi, bwana, ine ndikangolalikira chabe chimene Mulungu ayika pa mtima wanga, ndipo ndizo zonse.” Mukuwona? Ndipo ine ndikutsimikiza sizingakhale zimene iwo akuyesetsa kundipangitsa ine kuti ndiphunzitse. Kotero, maubatizo a utatu, ndi zina zotero monga izo, ndi kukangana nawo iwo. Ayi.

¹⁹ Koma ine ndafunsidwa ku msonkhano waukulu, ndi M’bale Boze. Iye wangokhala pafupi kubwera powona kuwala kwina kwa masana kwa chimene ife tikukhulupirira. Ndipo kotero ine ndafunsidwa kukalowamo ngati ndikupita paulendo wokusaka. Ngati iwo akandirola ine kulowamo, ngati ndikupita kokasaka... Ngati ine ndingamupeze wina woti akhoza kunditengera ine kokasaka, ndiye pamene ine ndikafike kumeneko, dotolo—dotolo ali kumeneko ku ofesi ya kazembe, ndi mzanga wapamtima kwa ine, wochokera ku Chicago. Ndipo ine ndikakangofika kumeneko, iye akati, “Chabwino, apa pali M’bale Branham cha apa. Tiyeni tikhale ndi msonkhano.” Kotero, ine nditafika kale kumeneko, ofesi ya kazembeyo siyingandiletse ine. Ngati iwo... Kotero iwo akuyesetsa kukonza zimenezo tsopano. Kotero ine ndikudalira kuti izo... Ngati chirichi chifuniro cha Mulungu, izo zichitika mwa njira imeneyo. Mukuwona? Izo—izo zaperekedwa chabe kwa Iye. Ngati ayi, ndiye ine ndidzakuzi witsani inu. Ine sindidza... .

²⁰ Ngati icho chikhala chifuniro cha Mulungu, ndiye, ine ndikufuna ndilankhule pa Malipenga Asanu ndi awiri. Ndipo uwo udzakhala pafupifupi ulaliki wa masiku asanu ndi atatu, ndipo ife sitidzakhala kuno ku Kachisi, mwina. Iye tikuyesa kupeza nyumba yolankhuliramo kuno.

²¹ Tsopano ine sindinaganizirepo, za nyumba iyi yatsopano yolankhuliramo imene yangomangidwa kumene kuno, iyo ili penipeni pamene ine ndinamuwona Yesu nthawi yoyamba m’masomphenya. Tsopano iyo yamangidwa, nyumba yolankhuliramo yamangidwa pa malo womwewo. Ine ndinapita pomwepo tsiku lina, kukawona. Pamene ine ndinayang’ana ndi kumuwona Iye akuyang’ana choloza kum’wawa, inu mukukumbukira kundimva ine ndikunena izo, pamene ine ndinali kumeneko ndikupempherera bambo wanga; m—mnyamata wamng’ono, mlaliki wachinyamata chabe. Ndi pamene ine ndinamuwona Iye. Kusuntha, kuyang’ana pa Iye; Iye anali mutu Wake atawupotolokera kumbali kundibisira ine. Ine ndinapitirira kuyenda choyandikira, kukonza kumero kwanga, mu kathengo ka miraza. Ndipo ine ndinapenyetseta,

ndipo Iye sanatembenuke konse. Ndiye ine ndinayitana Dzina Lake, “Yesu.” Ndipo Iye anachewuka, anatambasula manja Ake, ndipo ndizo zonse zimene ine ndinakumbukira mpaka kutacha. Ndipo kotero ine ndinabwerera kuchokera ku tchirelo, motsatira ku kucha kwa tsiku.

Kotero mwina Ambuye andirola ine kulalika Malipenga amenewo uko. Kulikonse kumene kuli, chifuniro cha Mulungu chichitika.

²² Tembenuzani mu Mabaibulo anu tsopano, ku Yesaya makumi asanu- . . . mutu wa 53 wa Yesaya.

Tsopano, ife tikudalira kuti Mulungu adalitsa kuyesetsa kwathu kofowoka pakudza palimodzi m’ mawa uno. Ife tabwera kumene kuchokera ku Philadelphia, kumene ine ndinali pa msonkhano waukulu wa Full Gospel Business Men, ndi kumvetsera ku maumboni awo osiyana ndi zina zoterozo, cha kumeneko.

²³ Ndiye ine, pa msewu kumusi, ine ndinali . . . Billy Paul ndi ine, ndi Rebekah ndi msungwana wamng’ono wa a Collins, Betty Collins wamng’ono. Ndipo Billy ndi wokonda kugona kwambiri, ndipo Becky aliko bwino, ndipo kotero ine . . . Betty ndi ine timalankhula. Ndipo iye anali atakhala kumbuyo ndi Becky, mu mpando wakumbuyo. Ndipo ine ndinawona chinachake pa msewu, chikuchitika; ndipo, pamene ine ndinatero, chinachake chinandikhudza ine. Ndipo Betty, ngati iye ali muno, iye anazindikira kuti ine ndinasiya kulankhula ndi kuyamba kulemba chinachake. Ndipo pamene ine ndinapezera mutu wa m’ mawa uno.

²⁴ Tsopano tiyeni tiime pamapazi athu. Ngati ife . . . Tsopano ife timaima popereka ulemu kwa Mawu a Mulungu, pamene ine ndikuwerenga Yesaya mutu wa 53.

Ndani wakhulupirira uthenga wathu? ndipo ndi kwa yani mkono wa YEHOVA wavumbulukira? (Zindikirani, ilo ndi funso, kuyamba ndi kuyamba.)

Pakuti iye adzaphuka pamaso pake ngati mtengo wanthete, ndi ngati muzu womera mu . . . nthaka yowuma: iye alibe maonekedwe pena kukongola; ndipo pamene ife tidzamuwone iye, palibe kukongola kuti ife timukhumbe iye.

Iye ali wonyozedwa ndi kukanidwa ndi munthu; munthu wa chisoni, . . . wodziwa zowawa: ndipo ife tinabisala momwe zinaliri nkhope zathu kwa iye; iye ananyozedwa, ndipo ife sitinamlemekeze iye.

Zedi iye wanyamula chowawa chathu, ndipo wasenza zisoni zathu: komabe ife tinamuyesa iye wofooka, wokanthidwa wa Mulungu, ndi wosautsidwa.

Koma iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, iye anatunduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu: chilango cha mtendere wathu chinali pa iye; ndipo ndi mikwingwirima yake ife tinachiritsidwa.

Ife tonse ngati nkhoa tasochera; ife tapotolokera mmodzi aliyense ku njira yake yomwe; ndipo YEHOVA wayika pa iye kusaweruzika kwa ife tonse.

Iye anaponderezedwa, ndipo... anasautsidwa, komabe iye sanatsegule pakamwa pake: iye anabweretsedwa ngati nkhoa kokaphedwa, ndi ngati mwanawankhoa pamaso pa omsenga ake... wosalankhula, kotero iye sanatsegula pakamwa pake.

Iye anatengedwa kuchokera ku ndende ndi ku chiweruziro: ndipo ndani adzafotokoze m'badwo wake? pakuti iye analikhidwa mu dziko la amoyo: chifukwa cha zolakwa za anthu anga iye anakanthidwa.

Ndipo iye anapanga manda ake palimodzi ndi oipa, ndipo ndi olemera mu imfa yake; chifukwa iye sanachite chiwawa chirichonse, ngakhale m'kamwa mwake munalibe chinyengo.

Komabe kunamkomera YEHOVA kumtunduza iye; iye... anamuyika iye ku chowawa: pamene iwe uti udzapange moyo wake nsembe ya tchimo, iye adzawona mbewu yake, ndipo iye adzatalikitsa masiku ake, ndipo chomkondweretsa YEHOVA chidzapambana m'dzanja lake.

Ndipo iye adzawona za mavuto a moyo wake, ndipo adzakhutitsidwa: ndi chidziwitso chake antchito olungama ambiri adzalungamitsidwa... ambiri; pakuti iye adzanyamula kusaweruzika kwawo.

Chotero ine ndidzamgawira iye gawo palimodzi ndi otchuka, ndipo... adzagawana zofunkha ndi amphamvu; chifukwa iye watsanulira moyo wake ku imfa: ndipo anawerengedwa nawo olakwa; ndipo iye ananyamula machimo a ambiri, napanga mapembedzero chifukwa cha olakwa.

²⁵ Atate Mulungu, Mawu Anu ali Nyali, Kuwala kumene kumawunikira njira ya wokhulupirira aliyense kukafika mu Kukhalapo kwa Mulungu, pamene Iyo imatitenga ife ngati muuni m'dzanja lathu. Inu simunatipatse kokwanira kuti ife tikhoze kuwona kumapeto kuchokera kuchiyambi, ndipo, koma ine ndimayenda ndi chikhulupiro. Koma monga munthu akhoza kuyenda kupyola nkhalango ya mdima usiku, ndipo ndiko kumene ife tiri; nyali imene iye amanyamula, imangomuonetsa phazi ndi phazi. Koma njirayo, ngakhale ikutsogolera m'mwamba, yenda chabe ndi Kuunikako. Ndipo mulole Kuunikako kuwalire lero pa Mawu, kutitsogolera ife

phazi limodzi kuyandikira ku Ufumu wa Mulungu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

Khalani pansii.

²⁶ Phunziro limene ine ndikumverera kuti ndilankhule kwa osonkhana lero ndilo: *Mbambande*.

Zikhoza kuwoneka ngati zachilendo kutenga ku—kuwerenga Lemba monga chonchi, la—la chimodzi mwa zithunzi zotunduzidwa kwambiri ndi zithunzi zakupha za m’Baibulo, kuti pamene Baibulo likunena, kuti, “Wantchito wangwiro uyu amene anasautsidwa, ndi kutunduzidwa, ndi kung’ambidwa,” ndipo komabe nkutenga phunziro kuchokera pamenepo, ngati, *Mbambande*. Zachilendo kwambiri. Koma ine . . .

²⁷ Lingaliro langa likuganiza, mmawa uno, pamene ife tiri paulendo wobwerera, ine ndikutero, kwa zaka zingapo. Ine ndinaitanidwa kupita ku Forest Lawn, mu—mu California, kumtunda kwa Los Angeles. Cholinga changa choyamba kupitira kumeneko chinali kukayendera ma—manda a—a Aimee Semple McPherson, woyambitsa wa gulu la Foursquare. Ndipo ine ndinapita kwake—manda ake. Ndipo ngakhale ine—ine sindigwirizana ndi mkaziyo, ngati mlaliki, komabe, mu mtima mwanga, ine ndimapereka kuyamikira ndi kulemekeza pa—pa chomwe iye anayimira, mu—ora, ndi mazunzo ndi zinthu zimene iye anali kupyola nazo, ndipo mu nthawi ya kukhala kwake pansii pano. Ndiyeno kwake—mwana wake wokonedwa, amene ali bwenzi langa la pamtima, Rolf McPherson.

²⁸ Ndipo gulu la alaliki, ife tinapita kumeneko. Ndipo iwo . . . ife sitinakhale ndi nthawi yokalowa mu—m . . . mu—malo amene iwo amawotcherako mitembo, ndi kuyika—matupi mu bo—bokosi laling’ono pa mbali ya khoma.

²⁹ Ndipo m’menemo iwo ali nazo zinthu zina zapamwamba, monga ngati M’gonero Wotsiriza. Ndipo umo ndi mowalitsidwa ndi kuwala kwenikweni kwa dzuwa. Ndipo iwo—iwo ali ndi chotsekera chimene chimawapatsa iwo . . . Pamene iwo alowa mkati, kuwala kwake; ndiyeno pamene—pamene iwo ayamba kulankhula, umo mumachita mdima. Ndipo pakapita kanthawi monse mumakhala mdima, ndiyeno anthu amatuluka. Ndipo iwo onse amakhala ndi M’gonero.

³⁰ Ndipo mkazi yemwe anasunga chinsinsi cha m’mene angalimenyere galasi ili mpaka m’malo amenewo, chifukwa, kupanga zithunzi zimenezi, chifukwa, zi—zinabwera kudzera m’banja, kwa zaka zambiri mmbuyomo. Ndipo lusolo linangopatsidwa kwa anawo, ndipo mmodzi wotsiriza anali mkazi. Ndipo iwo anali kupanga chithunzi ichi. Ndipo pamene iwo anapita kukaumba ndi kuwocha ga—galasi, kuliphika ilo, cha Yudasi Iskarioti, icho chinaphulika. Ndiyeno iwo anachiyesa icho kachiwiri, ndipo icho chinaphulika kachiwiri. Ndipo iye anati, “Mwina Ambuye wathu sakufuna chithunzi cha

mdani Wao pambali pa Chawo.” Ndipo anati, “Ngati icho chiti chiphulike kachiwiri, ife sitichitsiriza chithunzichi.” Koma icho chinakhala nthawi imeneyo. Ndiye, indedi, icho chinali chinthu chokhudza, ndi m’mene zinthu zoterozo zikanachitika.

³¹ Koma, ndiye, chimodzi cha zinthu zazikulu chimene chinandisangalatsa ine mu Forest Lawn, chinali cha Michelangelo, wosema wopambana, cho—chosedmedwa cha Mose. Ndi cho—chomwe anachipanganso kumeneko, ndithudi. Icho sichiri chapachiyambi, koma chinali mba—mbambande yopambana chotero. Ndipo pamene ine ndinayima ndi kuyang’ana pa icho, ine—ine ndinachikonda icho, chinachake chimene chimawoneka ngati (chikuyimira) chiri ndi chinachake kwa icho.

³² Ine ndimakonda luso, mwabwino kwenikweni. Ine ndikukhulupirira Mulungu ali mu luso. Ine ndikukhulupirira Mulungu ali mu nyimbo. Ine ndikukhulupirira Mulungu ali mu chirengedwe. Mulungu ali paliponse. Ndipo chirichonse chimene chikutsutsana ndi chapachiyambi ndi chisokonezo. Mulungu ali mu kuvina; osati mtundu wa kuvina kumene inu mumachita kuno. Koma pamene ana a amuna ndi aakazi a Mulungu akhala mu Mzimu wa Mulungu, onani, ndiko kuvina. Koma monga ife timalimbana nacho mpaka 2 koloko m’*mawa* uno, kumtunda uko mu kanjira, ndicho chisokonezo chake.

³³ Koma, ichi, ndi mbambande yomwe Michelangelo anali nayo—anali atapanga, icho—icho chinamutengera iye chinachake kuti apange icho—icho. Iye anali munthu wopambana, ndipo chinamtengera gawo lalikulu la moyo wake, chifukwa iye anali zambiri, zaka zambiri mu kuchisema. Kungotenga thanthwe ndi la—la nsangalabwi, ndi kupitiriza kulisema ilo. Ndipo, onani, munthu yekhayo, wosema mwiniwakeyo, ali nacho m’*malingaliro* ake chimene iye akuyesa kuchita. Iye, iye ndi mmodzi. Inu mukhoza kupita ndi kunena kwa iye, “Iwe ukujogoderanji pa *mwalawo*?” Kwa wakunja, amene sakudziwa chimene chiri mu mtima wake, ndi zamkhutu. Koma kwa munthu, wosema mwiniwake, iye—iye ali ndi—ndi masomphenya m’*malingaliro* ake, a chimene iye akuyesa kupanga, ndipo iye akuyesa kutulutsa chimene iye ali nacho m’*malingaliro* ake mwa mawonekedwe a—a chosedmedwa. Ndicho chifukwa chake iye akuchikumba icho kuchokera pa matanthwe.

³⁴ Ndipo ichi, kuti uchite, iwe uyenera kuyamba molondola, poyambirira, ndipo iwe uyenera kutsata pateni. Mukuwona? Inu simungakhoze kutenga kachidutswa kakang’ono, ndi kuyamba nako, “Ife tichipanga icho *mwanjira iyi*; ayi, ine ndikukhulupirira. . .” Ayi, iye ayenera kukhala nayo pateni yeniyeni. Ndipo m’*malingaliro* ake iye ali nayo pateni iyo. Ndipo iye sangakhoze kusiyana ndi pateni iyo. Tsopano, pofuna kuchita ichi, iye anayenera kuchijambula m’*malingaliro* ake, chifukwa

ife tiribe zithunzi zenizeni za Mose, koma iye anayenera kukhala ndi chithunzi cha m'mutu mu malingaliro ake, cha chimodzimodzi chimene Mose anali.

³⁵ Tsopano, wosema weniweni ndi wodzozedwa, monga wandakatulo weniweni, kapena woyimba weniweni, wazing'wenyeng'wenye, chirichonse chimene chingakhale. Zenizeni zonse ziyenera kubwera mwa kudzoza. Michelangelo ayenera kuti anali nako kudzoza kwa chimene Mose anali kuwonekera kwenikweni. Ndipo iye anachigwira icho m'malingaliro ake, chomwe Mose ayenera kuti anali. Kotero iye anachiyala icho pa chidutswa chachikulu cha nsangalabwi iyi, kudula mwa pateni, ndi kutsitsira mmusi, ndi kuchitcherereza mmusi, mpaka iye anafika ku chithunzi chenicheni cha chimene icho chiyenera kuti chinali m'malingaliro ake.

³⁶ Ndiyeno pamene iye anachipanga icho chonse mwangwiro chotero, kuchotsa ngodya iliyonse, ndi malo onse atafufutidwa, ndipo maso ake kungokhala bwino, ndipo tsitsi lililonse, ndi ndevu, zonse basi momwe izo zinaliri, iye anayima patali ndi kuyang'ana pa icho. Ine—ine ndikuganiza za—za zambiri, zaka zambiri za ntchito yolimba, ndi m'mene iye anagwirira masomphenya omwewo nthawi yonse, m'malingaliro ake, a chimene iye amati achichite. Ndipo tangoganizani, masomphenya amenewo pa malingaliro ake kwa zaka zambiri, kuti akachipange icho kuwoneka chimodzimodzi basi kwa chomwe icho chinali! Iye anagwira masomphenya choyamba, ndipo momwe iye anayenera kugwira ntchito kwa masomphenya awo, kudulapo ndi kupanga! Ndipo pamene iye anachifikitsa icho pamene iye anachipangitsa icho changwiro, mpaka icho chinakhaladi changwiro; iye anayima ndi kuyang'ana pa icho pamene iye anachitsiriza m'mawa uja, ali ndi nyundo m'dzanja lake.

Ndipo iye anadzozedwa kwambiri pamene iye anayang'ana pa icho, chifukwa masomphenya a m'malingaliro ake anali atayima patsogolo pake, mu chenicheni. Chimene iye anali atawona, ndipo... llingaliro lake la chomwe Mose anali, apo icho chinawoneka pamaso pake, chimene iye anali nacho mu mtima wake zaka zonse izi. Za kuvutika, ndi maora a chisoni ndi kupsyinjika, ndi osinjirira, ndi china chirichonse, komabe iye anakhala nawo molondola masomphenya mpaka icho chinatsirizidwa.

³⁷ Ndiyeno pamene icho chinatsirizidwa, iye anayima m'mbuyo ndi nyundo, kapena nyundo ya wosema, mu dzanja lake, ndipo iye anayang'ana pa chosedmedwacho. Ndipo kudzoza kwa masomphenya amene iye anali atawawona, a m'mene angachichitire icho, zinamudzoza iye mochulukwa kwambiri mpaka iye... Kudzozako kunamukhudza iye mpaka iye sanasamalire za wina, ndipo anachikantha icho pabondo, ndi kunena, "Lankhula!"

³⁸ Tsopano pali chilema pa chifano chopambanacho, pa bondo, pa bondo lakumanja. Pamwamba chabe pa bondo, pafupi mainchi asanu ndi imodzi, pali malo (ine ndinayika dzanja langa pamenepo) pafupi kuya *chonchi*.

³⁹ Atatha iye kutaya nthawi yonseyo, kwa zaka ndi zaka, kuti apange ichi; ndiye pansi pa—chikopa cha kuwona kukwaniritsika chimene iye anachiwona mu mtima wake ndi mu masomphenya ake, ndipo anakhumba kuchiwona, icho chinatsirizidwa. Ndipo pamene icho chinatsirizidwa, iye anadzozedwa nacho kwambiri mpaka iye anaganiza mbambande yake yomwe iyenera kulankhula kwa iye. Ndipo iye anachikantha icho pa mwendo, ndi kufuula, “Lankhula!” Ndipo iko kunapanga chilema pa icho. Iko kunayika chilema pa fanolo.

⁴⁰ Kwa ine, chilema chinali chimene chinapanga icho kukhala mbambande. Tsopano, mwinamwake kwa li—lingaliro limene lingaganize mosiyana, inu mukuganiza iko kunachiwononga icho. Ayi, kwa ine, iko—iko kunapangitsa icho chimene icho chinali. Icho—icho, chifukwa cha zaka zambiri za ntchito yogwiridwa mosamala ndi kuvutika, ndi kudzoza, ndi zina zoterozo, pochipanga icho, kuvutika kwake kunatsimikiziridwa kuti sikunali pachabe. Icho chinali changwirowo, ndipo ndicho chifukwa chake iye anafuula, “Lankhula!” Chifukwa, iye anali atawona pamaso pake kuti iye (anali) anali atakhoza kukwanitsa, kubweretsa pokwaniritsa masomphenya amene anali m’malingaliro ake. Ndipo chotero, pansi pa kudzoza, iye anachita chinachake mosaganizira, osati mwa wamba. Iye anachikantha icho, ndi kufuula, “Lankhula!” Onani, iye sakanachita icho ngati iye akanakhala ataganiza. Koma iye sanaganizire. Uko kunali kudzoza kwa kuwona chimene iye anali nacho m’malingaliro ake chitakhala pamenepo mwangwirowo pamaso pake.

⁴¹ Kuvutika kwake, ndi zolemetsa, ndi mausiku aatali, ndi kukhala kutali ndi zamdziko kwa masiku, ndipo mwina kudya kasangweji. Ndi—ndi kukhula pa icho, ndi kubwerera m’mbuyo, ndipo, “Ayi, umo si momwe icho chinaliri kumene. Tsopano chiyenera kubwera pansi ku *ichi*,” ndi kuchikhula icho. Ndiye pamene iye anachiwona icho, changwirowo basi, ndiye iye anachiwona mu chenicheni. Mthunzi wa chimene chinali mu malingaliro ake chinali chitakhala chenicheni, icho chinakhala chenicheni, chotero icho chinamudzidzimutsa iye. Ndipo icho chinali chenicheni kwambiri mwakuti iye anayenera kufuula, “Lankhula!”

⁴² Kwa ine, icho chinali chinyezimiro. Icho chinali—icho chinali chiyamikiro kwa ntchito yake, kuti ntchito yake yomwe inamudzozza iye kwambiri, mwakuti iye akanakhoza kufika posaganizira za wina nkuchimenya icho ndi kunena, “Lankhula!”

⁴³ Ine ndinayima pamenepo ndi kuyang'ana pa chosemedwacho. Ine ndinaganizira za maora amene munthuyo ayenera kuti anawayika, mu kupanga icho. Iwo ananena zaka zingati zomwe zinali. Koma icho—icho chinali chinyezimiro kwa iye, chifukwa icho chinali chothandizira ku lake—ku luso lake lalikulu, ntchito yake yayikulu ya chimene iye anali kuchita. Ndipo pamene iye potsiriza anali wokhoza kuchikwanitsa icho, icho chinali chopambana kwambiri.

⁴⁴ Tsopano tiyeni ife titembenuze tsamba, la Michelangelo, ndi kutseka bukhu.

Ndipo tiyeni titsegule Bukhu lina ndi kuwerenga za Wosema Wamkulu, Wamphamvuzonse. Yemwe, pasanakhale dziko, ndipo pasanayikidwe maziko, Iye anali nacho m'malingaliro Ake a chimene Iye ankafuna, ndipo Iye ankafuna kupanga munthu m'chifaniziro Chake Chomwe. Iye ankafuna kupanga chinachake mwa—mwa chenicheni cha chimene chinali masomphenya kwa Iye, chimene chinali mu kuganiza Kwake.

⁴⁵ Tsopano, kwa Michelangelo, chimenecho chinali chotsatira cha ganizo lake.

Ndipo Mulungu ankafuna kupanga munthu mwa chifaniziro Chake, Wosema Wamkulu, ndipo Iye anapita kukagwira ntchito pa iye. Ndipo ife tikuzindikira pamene Iye anabweretsa kuchokera ku zipangizo. Choyamba mwina chinali nsomba, ndipo kenako mbalame, ndipo—ndipo kenako zinthu zokwawa pa dziko lapansi, ndi—ndi zinthu zambiri zimene Iye anabweretsa. Koma, potsiriza, pamene Iye anafungatira, pokhala Mlengi, Iye anali...Iye sanali monga munthu, tsopano, wosema amene ayenera kutenga chinachake chimene chalengedwa, kuti aseme chifano. Iye anali Wosema wa zinthu Zamuyaya. Iye anali Wosema amene akanakhoza kulenga ndi kubweretsa mu kukhalapo icho chimene Iye anali nacho mu lingaliro Lake kuti achipange. Kapena, mwinamwake, Iye akhoza kupanga chopangira chimene malingaliro Ake anakhumba.

⁴⁶ Ndipo pamene Iye akuyamba kugwira ntchito pa zinthu zokwawa, monga pa—pa—pa nyama zazing'ono pa dziko lapansi. Ndiyeno Iye anayamba kuchibweretsa icho kuchokera pa icho kukhala chinachake, chapamwamba. Ndiye potsiriza Iye anachifikitsa icho ku nyama zazikulupo, monga ngati mkango, nyalugwe, chimbalangondo. Ndiye Iye anachifikitsa icho mu—mu—m'moyo mwinamwake wa—wa ankhwere ndi anyani, ndi zina zotero. Tsopano, osati kusinthasinthu, monga ife tikuganizira kuti china chinachokera ku...Icho chinali chirengedwe chathunthu; Mulungu akugwira ntchito mwa dongosolo.

⁴⁷ Koma potsiriza apo panadza pa dziko lapansi, ungwiwo, ndipo ameneyo anali munthu. Ndiyeno Iye ankakhoza kuwona

mwa munthu uyo, kuti ankawoneka monga Iye. Kotero tsopano pamene Iye anayang'ana pa iye, iye anali chinyezimiro cha chomwe Mlengi wake anali. Mulungu anali tsopano atakhoza kukhala nacho chinthu chimene Iye ankachifuna, munthu mu chifaniziro Chake chomwe.

⁴⁸ Ndiyeno ine ndikhoza kunena, kwa ichi, kuti, pamene Iye anamupanga munthu uyu, panali chinachake za iye komabe icho sichinkawoneka bwino basi, chifukwa kuti iye—iye anali mwa yekha. Ndipo umo ndi momwe Mulungu analiri, mwa Iyeyekha; Iye anali Wamuyaya. Ndipo munthu tsopano, mu chifaniziro cha Mulungu, nayenso anakhala pa dziko lapansi mwa iyeyekha. Kotero Iye ayenera kuti anakantha nk'honya pang'ono cha pa mbali yake yakumanzere, ndipo kuchokera pamenepo Iye anatenga kagawo kamene kanachoka pamenepo ndipo anamupangira iye womuthandizira, mkazi, ndiye iye sanali mwa yekha. Iye anali—iye anali, iye anali ndi winawake naye. Ndipo ndiyo ntchito Yake yayikulu.

⁴⁹ Ndipo, Iye, monga wosema wamkulu aliyense akanatenga yake—yake—mbambande yake . . .

Tsopano, poyamba, Iye anali nayo mbambande ya Iyemwini. Koma tsopano Iye anawona kuti mbambandeyo inali yosungulumwa, monga Iye analiri, kotero Iye anagawaniza mbambandeyo poyikantha iyo mu mbali ndi kutulutsamo womuthandizira.

⁵⁰ Ndipo tsopano, kuti apange awiriwo m'modzi, Iye anawayika iwo, monga wosema wamkulu aliyense, mu malo amene—amene ali okongola.

Wo—wosema sakanakhoza kupanga mbambande yopambana, ndiyeno nkuyitenga iyo ndi kukayiyika iyo mu kakhwalala penapake, kapena kuyibisa iyo kuseri kwa nyumba. Monga Ambuye athu anatiwuzira ife, “Munthu samayatsa muni ndi kuwuyika iwo pansu pa mbiya.” Pamene ife tikhala mbambande za Mulungu, ife sitibisala mu kakhwalala kwinkawake. Ife—ife tiyenera kupereka Kuwala.

⁵¹ Kotero ife tikuwona kuti—kuti Iye, Iye atatsiriza kupanga mbambande iyi, Iye anayiyika iyo apa pa dziko lapansi, ndi kuyiyika iyo mu malo okongola kwambiri amene analipo, m'munda wa Edeni. Iye anakhazika mbambande Yake, awiriwo pokhala m'modzi, m'munda wa Edeni. M'mene chiyenera kuti chinamkomera Iye, kuti Iye anawona mbambande iyi inali bwino. Iye, zitatha izo, ife tikupeza kuti Iye anapuma; Iye anakondwera nayo bwino ntchito Yake.

⁵² Tsopano kumbukirani kuti, lingaliro langa, mbambande ndi kukantha kumene kunawononga mbambande ya Mose wa Angelo Woyera mu chosema.

Ndipo kunali kukantha kumene kunadula mbali ya mbambande Yake, kumene kunaturutsamo mkwatibwi. Ndipo

tsopano ife tikuwaona iwo monga banja la mbambande m'munda wa Edeni. Zinali zokongola chotani izo! Ndipo icho chinamkondweretsa Iye, mpaka Iye—Iye anapuma ndiye. Iye anati, “Ine, ine ndipuma.”

⁵³ Koma pamene Iye anali akupuma ndi kudalira kwa mbambande Yake, m'dani Wake anadzamo ndi kuyipeza mbambande yopambana iyi. Ndipo iye, mwa chinyengo, iye—iye anakwawira pansu pa—pa makoma a m'munda, ndiyeno iye—iye anawononga mbambande yokongola iyi. Iye—iye anayiwononga iyo, kotero kuti iyo—iyo inagwa.

⁵⁴ Tsopano ine ndikuyesa kuyang'ana koloko iyo. Ndipo ine ndinamufunsa Mike, mdzukululu wanga, kuti alize belu lija mu maminiti makumi atatu, koma ine . . . Iye sanachite icho, ndipo ine ndakhala kale maminiti makumi atatu. Koma, ndiyo, ife tipitiriza pang'ono chabe. Mwaona? Tsopano, ine sindikufuna ku—kuswa malamulo awa. Ine—ine ndinawapanga malamulo amenewa, onani, ndipo ine—ine . . . ndipo apa pali kuswa lamulo lako lomwe.

⁵⁵ Tsopano zindikirani, ndiye, mbambande iyi. Pamene Satana anayigwira iyo, wonyengayo, anathyola kupyola m'zipupa, ndipo—ndipo iye anawononga mbambande iyi. Chifukwa chakuti njira imene Iye anachitira icho, chimene . . . Kodi iye anachita motani icho? Ine ndipita mwatsatanetsatane wa izo. Momwe iye anachitira icho, inali . . . Mbambande iyi inatetezedwa ndi Mawu, Mawu a Mulungu. Ndipo mbambande, iyomwini, ya banja, inatetezedwa ndi Mawu awa. Koma mbali yothyoledwa, imene inathyoledwa kuchokera ku yapachiyambi, inatuluka mpaka kuseri kwa khomalo, izo zinampatsa Satana mwayi kuti ayiwononge iyo. Ndipo tsopano monga inu mukudziwa chimene ine ndimakhulupirira pa zinthu zimenezo, kotero ine sindisowa kunena izo. Koma mbambande inaswedwa.

⁵⁶ Koma Wosema wamkulu, pamene Iye anawona kugwa kwa banja Lake, mbambande, Iye sanali wololera kungoyisiya iyo itagona pamenepo, chafufumimba, ndi kuwonongeka. Iye anapita kukagwira ntchito, mwamsanga, kuti ayimange iyo kachiwiri. Iye sanali kulolera kuti iyo iwonongeke, igone pamenepo monga choncho nthawi yonse. Chifukwa, Iye ndi Mulungu, ndipo Iye sadzagonjetsedwa. Kotero Iye anapita kukagwira ntchito mwamsanga ndi kuyamba kumanga kachiwiri mwa chifaniziro Chake Chomwe, munthu.

⁵⁷ Tsopano, ife tikupeza kuti dziko la chigumula linadza motsatira ndi kuwononga chinthu chonse, chifukwa mapangano amene anapangidwa, anapangidwa mwamangawa, “Ngati iwe sudzachita *ichi*, kapena ngati iwe udzachita *icho*.” Mulungu, Wosema wamkulu, anawona kuti munthu sakanakhoza—sakanakhoza kusunga pangano. Iye sangakhoze chabe kuchichita icho. Palibe chabe njira konse.

Pa kulankhulana mphindi zingapo zapitazo ine ndinali kulankhula kwa munthu m'chipinda, amene ali pano tsopano. Nati, "Koma, M'bale Branham, ine ndiri nazo zinthu zochuluka kwambiri zimene ine—ine ndikudziwa ziri zolakwika," ndipo m—mkazi wamng'ono waumulungu.

⁵⁸ Ine ndinati, "Koma—koma, yang'anani, mlongo, inu musamaziyang'ane pa inueni. Ndi chimene inu mukukhumba basi ndi chimene inu mukuyesa kuchita. Ndipo ngati inu mukumukonda Ambuye kwenikweni, inu mumayesa kumutumikira Iye ndi mtima wanu wonse, ndiyeno zolakwitsa zanu zonse zabisika mu Magazi a Ambuye Yesu." Mukuwona? Onani, Iye anapanga njira.

⁵⁹ Koteru Iye akuyamba tsopano, kumutenga munthu kuchokera ku mapangano Ake, o—onena kuti, "Ngati iwe udzati, Ine ndidzati." Ndipo Iye akuyamba ndi munthu wotchedwa Abrahamu, ndi kupereka kwa Abrahamu pangano, mopanda mangawa. Nthawi zonse Iye akayamba mbambande, Satana amayipeza iyo, chifukwa Mawu . . . Koma pamene Iye anayamba ndi Abrahamu, Iye anati, "Ine ndachichita kale icho. Tsopano ili ndi lopanda mangawa, osati chimene . . . kuti—kuti, 'Ngati iwe udzati, Ine ndidzati,' koma Ine ndachichita kale icho." Tsopano Iye, wo—Wosema, watsimikiza kuti akhale nayo mbambande iyi.

⁶⁰ Ndiye, kuchokera pa Abrahamu, kunadza mbadwa. Ndipo mbadwazo kwenikweni . . . Tsopano Mulungu akuchita chiyani? Iye akuyimanganso mbambande iyi imene inali itagwa. Koteru, mwa mbadwa, woyamba yemwe ife tikumupeza anali Abrahamu.

⁶¹ Tsopano penyani, mbambande iliyonse ikuyikidwa pa maziko, chosema. Chosemedwa ndi Angelo cha Mose chiri pa zitatu- kapena thunthu la nsangalabwi ya mapazi-anai. Ichu chiri ndi maziko. Koteru, Mulungu, mu kukonza mbambande iyi, Iye anayiyika iyo pa maziko a mbadwa. Ndipo maziko a mbadwa, woyamba, anali Abrahamu, kenako Isake, kenako Yakobo, kenako Yosefe, ngodya zinayi.

⁶² Ndipo, tsopano, Abrahamu anali maziko a chikhulupiriro. Tiyeni tine kuti iyo inali ndi maziko anayi. Maziko a chikhulupiriro anali Abrahamu. Maziko a chikondi anali Isake. Maziko a chisomo anali Yakobo, chisomo cha Mulungu kwa Yakobo; aliyense akudziwa izo. Koma mwa Yosefe munali ungiro, apo ndi pamene Iye akanakhoza kuyimitsa chosemedwacho; osati pa maziko woyamba, maziko achiwiri, maziko achitatu, koma pa maziko achinayi.

⁶³ Abrahamu anawonetsera Khristu, indedi; koteronso Isake, mu chikondi. Abrahamu anachita, mwa chikhulupiriro; Isake anachita, mwa chikondi; Yakobo anachita, mwa chisomo Chake. Chifukwa, *Yakobo* amatanthawuza "wonyenga," ndipo ndicho chimene iye anali, koma chisomo cha Mulungu chinali ndi

iyе. Koma pamene izo zinafika kwa Yosefe, palibe chirichonse chomutsutsa iye, pokandika pamodzi basi papang'ono, pakuti maziko ayenera nawonso kukhala mbambande. Pamene iye anawafotokozera atate ake, m'neneri, "Nenani kwa Farao kuti anthu anu ali—ali oweta ng'ombe ndipo osati oweta nkhosa, chifukwa woweta nkhosa ndi chonyansa kwa Aigupto."

⁶⁴ Koma pamene m'neneri wokalambayo anafika pamaso pa Farao, iye anati, "Antchito anu ndi oweta ziweto," Kotero icho chinaikanda iyo, mwawona, ndicho chifukwa chake iyo ikupangitsidwabe kukhala mbambande.

⁶⁵ Tsopano maziko akhazikidwa, kudzera mu chikhulupiro, chikondi, chisomo, ndipo ku ungiwiro, kupyolera mwa mbadwazo.

⁶⁶ Tsopano ntchito ya chimango imene inadza pa mbambande yopambana iyi inali aneneri, amene anali Mawu. Ine ndikuyembekeza inu mukhoza kuwerenga icho. Mukuwona? Aneneri; osati malamulo! Aneneri, pakuti aneneri anali Mawu otsimikiziridwa amene akupanga thupi; osati mbadwazo. Aneneri, iwo anali Mawu.

⁶⁷ Potsiriza, monga Iye anayambira mmbuyo momwe mu masiku a Mose ndi kubwera mmusi kudzera mwa aneneri, kwa mmodzi aliyense. Ndipo, potsiriza, kumanga chokweza thupilo, kuyandikira nthawi zonse. Ndipo wopambana wa onsewo anali Yohane. Baibulo linanena choncho. Yesu ananena izo. "Palibe munthu, amene anabadwapo mwa mkazi, wopambana ngati Yohane M'batizi," pakuti iye anali yemwe akanakhoza kulozera Mawu.

⁶⁸ Ndiyeno panadza, potsiriza, Mutu wopambana, Mutu wa izo zonse. Thupi lonselo limangolankhula za Iwowu. Maziko anakhazikitsidwa ndi mbadwa; koma thupi linamangidwa ndi Mawu, amene anali aneneri; ndipo apa pakubwera Mutu wa izo zonse, Yesu anadza powonekera. Pamene, pamene chigawo cha Mutu ichi chinayikidwa pa iyo, ife tikupeza mwa Iye ntchito ya manja yonse ya Mulungu. Ife tikupeza mwa Iye chinyezimiro changwiro cha Mawu, pakuti Iye anali Mawu, chidzalo cha Mawu. Tsopano, kachiwiri, Mulungu ali ndi Mbambande yangwiro panonso.

Monga Yesaya ananena, "Taanani Wantchito Wanga, Mbambande Yanga, imene ine ndayiwonetsera popyola m'mibadwo yonse ya Mmodzi wangwiro wakudza uyu. Ndipo apa Iye wayima pamaso Panga kumene, wangwiro!" Apo, mu chifaniziro Chake Chomwe, kunyezimiritsa Mulungu! Pakuti Iye ananena, mu Yohane Woyera 14, "Pamene inu muwona Ine, inu mukuwona Atate."

⁶⁹ Ndipo, ndiye, "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu," ndipo Mawu anadulidwa nanyezimiritsa chimene Mawu anali pachiyambi. Iye, Mawu, ananyezimiritsidwa

mu Mbambande mwa chifanizo Chake Chomwe, Mulungu kubwereranso mwa kufanana Naye Kwake, maonekedwe a Mawu akunyezimiritsidwa mu fano la munthu, Mbambande.

⁷⁰ Aneneri onse anali nazo zilema; onsewo anali kagawo. Koma apa, potsiriza, kubwera mmwamba kupyola mu izo, potsiriza pakudza Mbambande, Mmodzi wangwiro, wopanda cholakwika mwa Iye konse, wonyezimiritsidwa mwangwiro zedi wa Mwiniwake Womangayo, fano Lake Lomwe linanyezimiritsidwa mu ntchito Yake. “Mulungu ndi Khristu anali M’modzi,” mwakuti mpaka Iye anayika Mzimu Wake Womwe mwa Iye, ndiyeno ngakhale fano ndi Womanga anakhala Mmodzi. Mulungu ndi ntchito Yake yosedmedwa, Mbambande Yake! Kumene Mose—Mose anali, mu ntchito ya Angelo Woyera, anali . . . kapena Michelangelo, kani; inali—ntchito yosedmedwa imene inali yakufa, chifukwa icho chinapangidwa kuchokera ku mwala. Koma apa, Katswiri Womanga, pamene Iye anapanga ntchito ya manja Ake kukhala yangwiro, Iye analowa mkati mwa Iyo.

⁷¹ Wopangidwa mwangwiro kwambiri Woombola wa anthu, wangwiro kwambiri, waumulungu kwambiri; komabe, apo panalibe kukongola koti ife timukhumbe Iye. Pamene Mwana uyu wobadwa mwa namwali wa Mulungu wamoyo anakhala wangwiro kwambiri, ndi wodzichepetsa, ndi mu chifaniziro cha Mulungu, mpaka Mbuye wamkulu Amene anali atabweretsa Moyo Wake kupyolera mwa aneneri . . . Ndipo Iye anali chikwaniritso cha aneneri onse. Iye anali wangwiro kwambiri, mpaka, Mulungu powona ichi, Iye anamukantha Iye ndipo anafuula, “Lankhula!” monga Michelangelo anachitira, “Lankhula!”

Inu mukuti, “Kodi ziri choncho?”

⁷² Marko Woyera 9:7, ife tikupeza, pa Phiri la Mawalitsidwe, pamene apo panayima Mose, lamulo, apo panayima Eliya, aneneri. Njira yonse mmbuyo kuchokera kwa mbadwa, makolo, chilamulo, aneneri, ndi ena onsewo atayima pamenepo. Ife tikumva Liwu likubwera pansu kuchokera mu mtambo, ndi kunena, “Uyu ndi Mwana Wanga wokoneddwa; mvereni inu Iye!” Ndipo ngati iwo ati akamve, Iye ayenera kulankhula. Anali chabe masiku pang’ono Iye asanakanthidwe. “Uyu ndiye Mwana Wanga, Amene ine ndikukondwera kukhala mkati mwake. Ine ndamuwumba Iye. Ine ndakhala zaka zikwi zinai kuti ndimufikitse Iye ku ichi. Ndipo tsopano, Iye ali wangwiro kwambiri, Ine ndiyenera kumukantha Iye koteru Iye akhoze kulankhula. Mvereni inu Iye! Iye ndi Mmodzi wangwiro. Iye, Iye ndi Mbambande.”

⁷³ Kumbukirani, Iye anawonetseredwa nthawi zonse, mmbuyo kupyola Chipangano Chakale.

Ife tikumupeza Iye monga Thanthwe mu chipululu, limene lanakanthidwa, Thanthwe mu chipululu. “Ine ndine Thanthwe lija limene linali mu chipululu.” Koma uwo unali mwala umene unali usanafikebe ku ungiro wake. Koma mwa mawonekedwe oyimira Ilo linatsata mpingo, kukatunga kuchokera mwa Ilo icho chimene Iye akanakhoza kutunga, kupereka Moyo kwa iwo Amene Iye akanakhoza kuwapatsa Moyo. Koma Iye anali Thanthwe lija mu chipululu. Iye anali asanapangidwebe kukhala munthu. Iye anali kokha mu choyimira.

⁷⁴ Mose anamuwona Iye atayima pa Thanthwe ili. Iye anamuwona Iye akudutsa pafupi, ndipo iye anati, “Ndi gawo la msana wa munthu.” Inu mukuwona, Wosema anali kuwonetsa kwa Mose, chimene chinali chifaniziro cha Khristu mwakungolankhula, chimene Mbambande yopambana ikanamadzaoneka monga pamene Iyo idzafika pa ungiro. Iye anadutsitsa Yake...Iye analowetsamo, kapena—kapena anawonetsera kwa Mose masomphenya a chomwe Mbambande ikanamadzaoneka ngati. Ilo linali gawo la msana wa munthu, pamene Iyo inadutsa pafupi mu chipululu.

⁷⁵ Kumbukirani, Angelo anangokhoza kufuula ndi kukantha fano, ndi kunena, “Lankhula!”

Koma zinali zosiyana chotani kwa Mulungu, Wosema wamkulu. Pamene Iye anapanga munthu m’chifaniziro Chake Chomwe, mwangwiro kwambiri koti Icho chinanyezimiritsa Iye, Mulungu analankhula kupyolera m’chifaniziro cha munthu, kuwonetsera chimene Iye akanadzachita. Iye analankhula kupyolera mwa aneneri pamene iwo anali m’chifaniziro mwakungolankhula, pamene Iye anali kuchibweretsa icho mpaka ku Mutu. Koma pamene Iye anadza mu Mutu, Iye anali chifaniziro chonse cha Mulungu; Iye anali kudziwonetsera Iyeyekha. Ndiye, atakanthidwa chifukwa cha ife, tsopano Iye ali Mbambande kwa ife, Mphatso ya Mulungu, Yesu Khristu, Moyo Wamuyaya. Ine ndikuyembekeza kuti ife sitiwiwala konse izo.

⁷⁶ Pamene ife tikuwona masiku akudetsedwa, pamene ife tikuwona mithunzi ikugwa! Pamene, ine ndikuneneratu, “Kwangotsala kuzungulira kungapo kwina kwa dzuwa. Fuko lino lapita.” Kodi inu mukudziwa... .

Dzulo, 4 wa Julaye. Thomas Jefferson anasayina chikhazikitso cha ufulu, iye ndi bungwe limene linali ndi iye, ndipo Belu la Ufulu linalira, ndipo ife tinatchedwa oyima patokha, monga fuko. Malingana ndi mbiriyakale, sipanakhalepo demokarase pa nthawi iliyonse inatha kuposa zaka mazana awiri. Ndipo iyo inali 1776, Julaye pa 4. Ndipo ife tangotsala zaka khumi ndi chimodzi. Kodi zidzatheka? Ayi, sizingakhoze, mwawona. Zaka khumi ndi chimodzi. Ndipo, ngati izo zichitika, izo zidaswa mbiriyakale yonse.

⁷⁷ Ndipo ife tikuwona chikhalidwe cha nthawi. Ife tikuwona chikhalidwe cha anthu. Ife tikuwona chikhalidwe cha ndale. Ife tikuwona chikhalidwe cha dziko. Ilo silingakhoze kuyima. Ilo liyenera kumira, monga Titanic. Ilo liyenera kupita pansu, pakuti lawo likupereka malo. Fuku limodzi limapereka malo kwa lina, pamene ilo likugwa. Ndipo ufumu uno uyenera kugwa, ndi maufumu ena onse, kuti apereke malo kwa Ufumu uwo umene uli nkudza, umene sungakhoze kugwa. “Pakuti ife tikulandira Ufumu umene sungakhoze kusunthidwa,” kudzera mu chifaniziro changwiwo ichi cha Mulungu, Mbambande.

⁷⁸ Mulungu, pamene Mulungu anayang’ana pa Iye, Iye anadzodzedwa kwambiri! Iye anali chotero...kumuwona Iye momwe Iye ankawonekera, ndi kuwona ma—mawonekedwe a Iye, Iye anadzodzedwa kwambiri kuti iyo ingakhale Mbambande yangwiwo ya Wowombola, Yesu Wowombola. Kotero, Mulungu, pofuna kuti akanthidwe, Iyemwini; chifukwa, kuti alipire dipo Lake lomwe, Mulungu ndi Khristu anakhala Mmodzi, kotero kuti Mulungu akanakhoza kukanthidwa mu Chifaniziro, Iye akanakhoza kuvulazidwa. Ndipo ndicho chifukwa chake Yesaya anati, “Ife tinamuyesa Iye wokanthidwa ndi wosautsidwa wa Mulungu. Komabe Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, Iye anatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu yathu; chilango chotitengera ife mtendere chinali pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.”

⁷⁹ Chifaniziro changwiwo, Mulungu-Munthu! Mulungu, mwa *en morphe*, anali atasintha kuchokera ku Chauzimu kukhala masomphenya, ndipo masomphenya anakuzidwa nafika mu Chifaniziro. Ndipo Chifaniziro chinakanthidwa kotero kuti Chauzimu chikanakhoza kulawa kumverera kwa imfa, Mbambande yangwiwo ya Mulungu.

Iye sakanakhoza kuchichita ichi mwa Mose. Iye sakanakhoza kuchichita ichi mwa aneneri; Yesaya, amene anadulidwa ndi macheke mpaka iye anadulidwa mziduswa. Iye sakanakhoza kuchichita icho mwa aneneri amene anagendedwa. Iye sakanakhoza kuchichita icho, chifukwa Iye sakanachimverera icho; umo munangokhala gawo la Iye.

Koma mu Mbambande yangwiwo iyi, Iye anali chidzalo cha Umulungu mthupi. Iye sakanakhoza kuwonetsera Mose yekha; Iye akanawonetsera Uthunthu Wake wonse mwa Munthu uyu, ndi kulawa imfa chifukwa cha mtundu wonse wa anthu. Mbambande yangwiwo ya Mulungu! Mulungu, kudzodzedwa kwambiri pochuwona Icho, Iye anakhala Wowombola wa mibadwo yonse; kulankhulira iwo a m’mbuyo mwakemo, amene analipo kale, ndi tsopano.

⁸⁰ Malonjezo onse anadzakumanira mwa Iye. Iye anali Ungwiwo wa ungwiro. Zoyimira zonse zinakwaniritsidwa mwa Iye; Wowombola wathu Wachibale, mwa Rute ndi Boazi; Wotipatsa-

Malamulo wathu, kuchokera ku Phiri la Sinai; Mneneri wathu, wochokera ku chipululu, monga Iye anadza kuchokera m'phiri, monga Iye anadza kuchokera mchipululu; monga Iye anadza kuchokera ku Muyaya ndi kudzakhala munthu, Chifaniziro changwiro!

⁸¹ Mulungu, mmusi kupyola m'badwo, posema, mwa mbadwa, ndi kupanga nsanja Yake, ndi kuwabweretsa iwo kuchokera ku zinthu zosiyana kuti Iye akanayika maziko awa pamene. Pamene Iye anayamba kumangapo Mawu Ake, aneneri. Ndipo kenako, potsiriza, kubwera mpaka kwa Mneneri wangwiro, Maziko angwiro, masomphenya angwiro amene Mulungu anali nawo.

⁸² Ndipo tsopano, kuti ichi chilankhule, Iye ndi Mawu. Ndipo kuti Mawu alankhule, Iye ayenera kulowa mu Chifaniziro. Ndiyeno kuti Chifaniziro chilankhule, icho chiyenera kukanthidwa. Iye akudza mkati mwa Chifaniziro, ndiyeno polinga kuti chilankhule, Wowombola wangwiro.

⁸³ Zoyimira zonse za Chipangano Chakale zinakumana mwa Iye. Monga ine ndinanenera tsiku lina, Yehova wa Chipangano Chakale ali Yesu wa Chatsopano. Inde.

⁸⁴ Monga ambiri a inu, amuna, akazi, msinkhu wanga; ife tinali nawo, m'dziko monse, malo ambiri ochapirako zovala achi Chinese. Pamene achi Chinese oyamba anayamba muno, iwo anabwera kuchokera ku Gombe la Kumadzulo, kumasunthira chakum'mawa, kubwera kuno kuchokera ku dziko Lakum'mawa, kusunthira njira iyi. Ndipo pamene iwo anatero, iwo anali anthu amene anali osazolowera chinenero chatu ndi njira zathu, koma iwo anali anthu odziwa kuchapa. Ndipo iwo sankatha kulemba chiphaso kotero kuti iwe ukanakhoza kukatengera zochapitsa zako.

Koma, bambo wa Chichaina, iye anazipezera yekha mulu wa makadi aang'ono opanda kalikonse pa iwo konse. Kotero pamene iwe udza kudzachapitsa zako, iye amakhoza kutenga khadi ili naling'amba ilo mwa njira ina yake; nakupatsa iwe chidutswa chimodzi, ndipo iye ankasunga chidutswa chinacho. Ndipo, tsopano, ndi zabwino pang'ono kuposa zimene ife tiri nazo tsopano, chifukwa pamene iwe ubwerera kudzatenga chimene chiri chako, zidutswa ziwirizo ziyenera kulumikizana. Iwe sukanakhoza kubera icho ngati umati utero. Palibe njira imene ungachitire izo. Iwe ukhoza kulemba zilembo zofanana, koma iwe sungabere mang'ambidwewo. Icho chiyenera kugwirizana chimodzimidzi ndi chidutswa chinacho. Kotero, zovala zanu zakuda zimene munadza nazo, inu makanakhoza kuziwombola izo ndi chiphaso ichi, chifukwa icho chimalumikizana ndi chiphatso chimene chinaperekedwacho.

⁸⁵ Ndipo pamene Mulungu, mwa aneneri, ndi pansu pa chilamulo, anatitsutsa ife ku tchimo; ndipo lamulo liribe

chisomo, ilo limangokufotokozerani inu kuti inu ndinu ochimwa. Koma pamene Yesu anadza powonekera, Iye anali chikwaniritso, Iye anali—chikwaniritso cha chirichonse Mulungu analonjeza. Iye anali changwirowo, chifaniziro chofanana cha lonjezo. Kotero, malonjezo onse a m'Chipangano Chakale anadzakumana mwa Yesu Khristu. Izi sizikanakhoza kukumana mwa Mose, izi sizikanakhoza kukumana mwa aliyense wa aneneri, koma izi zinakumana mu Mbambande. Iyo inafanana ndi zonse zimene Icho chinanena kuti Iyo idzakhala.

Kotero Mpingo uyenera kukhala wofanana kwa chirichonse chimene Mulungu analonjeza. Iwo uyenera kukhala chidutswa chimene chakanthidwa kuchokera kwa Iyo. Kotero ngati chapachiyambi chiri Mawu, kotero adzakhala omvera amene atengedwa kuchokera kwa Iwo kukhala Mawu, kugwirizana ndi mbali Yake.

⁸⁶ Chotero, bambo wa Chichaina, inu mukanakhoza kutenga. . . Kumene, lamulo limakutsutsani inu ndipo linati inu munali onyansa, ndipo inu munali olakwa, ndipo akanakhoza kukuikani inu m'ndende. Koma pamene Iye anadza, Iye anali Chidutswa-chofanana chake, chimene chikanakhoza kukutengerani inu kunja; ndi kukubwezeretsaninso inu, ku—kukakhala chiphaso chathunthu, chiwombolo chimene Mulungu anali atalonjeza kale m'munda wa Edeni. “Mbewu yako idzaphwanya mutu wa serpenti. Koma, chidendene Chake chidzaphwanya—chidzaphwanya mutu wake.”

⁸⁷ Tsopano ife tikupeza Mbambande yangwirowo iyi imene Mulungu anayitsiriza. Tsopano, ife tikuzindikira kuti Iye anali chonse chimene chinalonjezedwa kuti chikhale. Iye ali malonjezo onse, zonse za mauneneri, chirichonse chimene Mulungu anapanga lonjezo lake. “Mbewu Yako idzaphwanya mutu wa serpenti.” Tsopano, Iye sakanakhoza kuuphwanya iwo ndi lamulo, Iye sakanakhoza kuuphwanya iwo ndi aneneri, koma Iye anachichita icho pamene Mbewu ya mkazi inakhala Mbambande, Khristu. Iye anali Mwala umene Danieli anawuwona utasemedwa kuchokera ku phiri. Iye anali Mmodzi akanakhoza kukantha. Iyeyo ali Mmodzi amene akanakhoza kuphwanya, kuphwanya mutu wa serpenti.

⁸⁸ Moyo wake unafanana, chimodzimodzi, moyo wa Mose. Moyo wake unafanana ndi Davide. Tiyeni tiwone ngati iwo unali, ngati Iye ali Chidutswa-chofanana.

⁸⁹ Zindikirani Davide, mfumu yokanidwa, pa anthu ake omwe. Iye anali. Tsiku lina pamene iye anali. . . Mwana wake yemwe anawuka momupandukira iye, ndipo iye analekanitsa ndi kugawa ankhondo a Israeli. Ndipo iye anali, Davide, anachotsedwa, kapena kuchotsedwa ndi anthu ake omwe, kuchoka pa mpando wachifumu wake.

Ndipo ali panjira yake, panali munthu wina amene anamuda iye, ndipo iye akuyenda pamenepo, kulavulira pa Davide. Mulonda uja anaturutsa lupanga lake, nati, “Ine ndisiye mutu wa garu uyo ukhale pa iye, kulavulira pa mfumu yanga?”

Davide anati, “Musiye iye yekha. Mulungu wamuwuza iye kuti achite izo.”

⁹⁰ Kodi inu simukuona? “Munthu wa nsoni, wozolowerana ndi zowawa. Iye akuyima ngati Nkhosa, pamaso pa oyisenga, chete.” Iwo . . . Iye ananena choncho. Mwina Davide sankadziwa chimene iye anali kunena.

Koma pafupi zisanu, zaka mazana asanu ndi limodzi mtsogolo, kapena zochuluka pang’ono, Mwana wa Davide anali akupita kupyola mu misewu yomweyo, ndipo Iye analavuliridwa. Koma zindikirani chimene chinachitika pamene, Davide, kuchokera mwa ake—kuchokera mwa ake . . . pamene iye anakhala wobisala; ndipo atachoka kothawira kwakeko, pamene iye—pamene iye anabwerera, munthu uja anapempha mtendere ndi chifundo. Ngakhale iwo amene anamukantha Iye adzamuwona Iye tsiku lina pamene Iye ati abwerere.

⁹¹ Ndipo ife tikupeza ndiye, mwa Yosefe, kuti Yosefe anali mnyamata wobadwa-modabwitsa, wotsiriza, gawo lapamwamba pa mazikowo, pamene mbambande inayenera kumangidwapo. Izo zikuchokera ku chikhulupiriro, ndi ku chikondi, ndi ku chisomo, izo zinabwera ku ungwiro. Ndiye chotero zinachita icho, kuchokera ku mapazi a kuyamba, kubwera mpaka ku ungwiro mwa Khristu. Zindikirani momwe Iye anawonetsedwera mwa Yosefe, pamwamba pa maziko, wangwiro kwambiri wa onse a iwo.

⁹² Ife tikupeza kuti Yosefe anabadwa ku banja lake. Ndipo iye anali mwa mkazi wovomerezeka, kwenikweni, amene anali mkazi wa Yakobo. Ndipo zindikirani, aponso, kuti pamene iye anabadwa, atate ake anamukonda iye; ndipo abale ake anamuda iye, popanda chifukwa. Chifukwa chiani iwo anamuda iye? Chifukwa iye anali Mawu.

Mukuona maziko omwe? Mukuona mmene mutu wa maziko unafikira? Tsopano, yang’anani pa Mutu wa thupi, ukudza. Tsopano penyani Mutu wa Mkwatibwi ukudza. Mukuona, Iye anali Mawu.

Ndipo iwo anamuda iye chifukwa iye anali mpenyi. Iye ankawoneratu zinthu, nawafotokozerana iwo. Izo zinkachitika. Zinalibe kanthu kuti zachedwa motalika chotani, izo zinachitika chimodzimodzi basi. Ndipo pakukhala wauzimu, iye anachotsedwa pakati pa abale ake. Iwo anayenera kukhala akumukonda iye. Koma iwo anamuda iye, chifukwa iye anali m’neneri ndipo iye anali wauzimu. Ndipo iwo anamuda iye.

⁹³ Zindikirani, iye anagulitsidwa kwa pafupi zidutswa za siliva makumi atatu; anaponyedwa mu dzenje, nayesedwa kuti wafa, koma anaturutsidwa kuchokera mu dzenje. Ndipo mu nthawi ya kuyesedwa kwake, mu ndende; wopereka chikho ndi wo—wophika mkate, ife tikudziwa kuti wopereka chikho anapulumsidwa ndipo wophika mkate anatayika. Ndipo m'nyumba ya ndende ya Khristu, pa mtanda, m'modzi anapulumsidwa ndipo mmodzi winayo anatayika; mbala ziwiri, awiri ochita zolakwa.

⁹⁴ Ndipo ife tikuzindikira iye anatengedwa kuchokera mu ndende yake, kupita ku dzanja la manja la Farao; mwakuti palibe munthu akanakhoza kulankhula kwa Farao, kupyolera mwa Yosefe yekha. Ndipo pamene Yosefe ankachoka pa mpando wachifumu wa Farao, ndipo lipenga linkalira mu Igupto monse, phokosolo limapitirira nati, “Gwadani bondo, aliyense, Yosefe akubwera kumeneko!”

⁹⁵ Chotero izo zidzakhala ndi Yesu. Momwe Iye anakonedwera ndi Atate, ndi kudedwa ndi iwo abale a chipembedzo, popanda chifukwa. Iye anagulitsidwa ndi zidutswa za siliva makumi atatu, monga zinachitikira; nayikidwa m'dzenje, kuyesedwa kuti wafa. Pa mtanda; m'modzi anatayika ndipo mmodzi winayo anapulumsidwa. Ndipo anakwezedwa m'mwamba kuchokera pa mtanda; ndipo akukhala ku dzanja lamanja la Mulungu, mu Ulemerero, Mzimu wopambana, umene unanyezimiritsidwa mwa Iye. Ndipo palibe munthu akhoza kulankhula kwa Mulungu, pokha kupyolera mwa Yesu Khristu. Ganizani za icho! Ndipo pamene Iye achoka pa Mpando wachifumu umenewo, kuyamba kuyenda, “Lipenga lidzamveka, ndipo bondo lirilonse lidzagwada ndi lirime lirilonse lidzavomereza.”

⁹⁶ Kumbukirani, iye anali mwana wa kupeza bwino. Chirichonse chimene iye anachita chinachita bwino. Ngakhale iyo inali ndende, kapena paliponse pamene icho chinali, icho chimadzatha bwino.

Ndipo Iye sanalonjeze kwa ana Ake kuti Iye adzachita chirichonse kuchita limodzi kwa ubwino. Ngakhale iwo anali matenda, nyumba ya ndende, imfa, zisoni, chirichonse chimene chinali, kuti icho chidzachitira ubwino kwa iwo amene amukonda Iye. Iye analonjeza izo, ndipo izo ziyenera kukhala choncho. Icho chiyenera kukhalapo. Ndi chophiphiritsa, chinalankhula kwa ife mwa Iye. Iye anali Chifaniziro changwiwo cha Mulungu. Tsopano ife tikuwona pano, naponso, kuti pamene Iye abweranso . . .

⁹⁷ Kumbukirani, Yosefe mwa vumbulutso anapulumutsa dziko, ndi uneneri wake wopambana. Dziko likanafa ngati iko kukanakhala kuti kulibe Yosefe.

Ndipo dziko likana—likanakhala litafa ngati kukanakhala kulibe Yesu. “Pakuti Mulungu anakonda kwambiri dziko, kuti Iye anapatsa Mwana Wake wobadwa yekha, kuti aliyense amene akhulupirira pa Iye asatayike.” Mulungu akusunga Moyo.

⁹⁸ Mopitirira pitirira ife tikhoza kupita! Chifukwa, Iye mophweka anali chofanana cha Davide. Iye anali chofanana cha Mose. Iye anali chofanana cha Eliya. Iye anali chofanana cha Yosefe. Chirichonse chiri chowonetseredwa kapena cholankhulidwiratu ndi Iye mu Chipangano Chakale, chinafanana mpaka mu icho, (ndi chiani icho?) kusonyeza Woombola wangwiro. Yemwe, ife tikanakhoza kuyikamo zovala zathu zakale zakuda mochapira, kupita kukazitenganso izo. Izo zachapidwa mu Mwazi wa Mwanawankhosa. Ife tikhoza kutenga zimene ziri zathu zomwe. Ndipo chirichonse chimene Iye anachifera, ife tikhoza kuchitenga icho. Koteru, Iye anali Mawu angwirowo, owonetseredwa.

⁹⁹ Ichu chinamkondweretsa Mulungu, Wosema wamkulu, kuti amukanthe Iye, ndi kuti achichite icho mwa njira iyi. Ife tikumuwona Iye mu Yesaya apa, monga ine ndinawerenga, “Ife tonse tinampenya Iye, ife tinabisa nkhope zathu kwa Iye. Panalibe kukongola kuti ife tikamkhumbwe Iye,” aliyense akukamba za Iye, kuchita zomutonga Iye. Ine ndikukamba za Iye tsopano mu tsiku ili, aliyense akuchita zomutonga Iye. Mukuona? “Ife tinampenya Iye, ife tinamuwona Iye.” *Esteem* amatanthauza “kuyang’anapo.” “Ife tinamupenya Iye wokanthidwa ndi wozunzidwa wa Mulungu.” Komabe, Iye, kodi Iye anachitiranji izi? “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; Iye anatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu.”

¹⁰⁰ Tsopano, ife tikanakhoza kumapitirirapitirira ndi izo, koma ine ndikukhulupirira inu muli ndi chithunzi cha chimene ine ndikutanthauza tsopano, Mulungu kumanganso Mbambande Yake.

¹⁰¹ Koma tiyeni ife tisaiwale kuti muchiyambi pamene Iye anakantha mbali ya Adamu, Iye anatenga chinachake kuchokera ku nthiti yake.

Tsopano, kukanthidwa kwa Khristu kunali kwa cholinga, kuti Iye akhoze kutenga kuchokera mwa Iye, mmodzi, woti akhale banja, Mkwatibwi; Iye akhoze kumtengera Iye Mkwatibwi. Koteru pamene Mbambande Yake inafika pa ungwiro, ndiye Iye anayenera kuyikantha Iyo, kuti atenge kuchokera mwa Iye; osati chidutsa china, osati chirengedwe china, koma cha chirengedwe chomwecho.

¹⁰² M’bale wanga, usaganizire moipa za ichi, koma taganiza kaminiti. Ngati Iye anatenga kuchokera mwa Iye, chirengedwe chapachiyambi, kuti apange Mkwatibwi wa Iye, Iye sanapange chirengedwe china. Iye anatenga gawo la chirengedwe chapachiyambi. Ndiye, ngati Iye anali Mawu, Mkwatibwi

ayenera kukhala chiani? Iye ayenera kukhala Mawu apachiyambi, Mulungu wamoyo mu Mawu.

¹⁰³ Kimberley, South Africa. Kamodzi ine ndinali kuyang'ana pa daimondi, momwe iye amachotsedwera kuchokera mu nthaka. Ndipo ine ndinamuwona iye ali pamenepo. Monga, chabwino, a—a kapitao wa makinawo, kapena wa m'godi, anali m'modzi wa othandizira anga mu mzera wa pemphero. Ndipo ine ndinazindikira daimondi, wokwana madola makumi zikwi, atawunjikidwa palimodzi, koma iye sanali kunyezimira ngakhale pansi pa kuwala. Ndipo ine ndinati kwa kapitawo wa mgodi, ine ndinati, "N'chifukwa chiani iye sakunyezimira?"

¹⁰⁴ Iye anati, "Bwana, iye sanadulidwebe. Iye ayenera kudulidwa. Ndiye, pamene iye wadulidwa, ndiye iye amanyezimiritisa kuwala." Ndi zimenezotu.

¹⁰⁵ Mbambande iyenera kudulidwa. Zindikirani, kudulidwa chifukwa chiani? Kodi chidutswa chimadulidwapo? Ai, ai. Kachidutswa kamene kadulidwako, iko kamapangidwa nidulo ya victrola, ndipo nidulo ya victrola imaikidwa pa—pa—pa rekodi imene ili ndi nyimbo yosaoneka kwa dziko. Koma niduloyo ndi imene imatulutsa iyo kunja, imaitulutsa kumasulira kowona kwa Mawu.

¹⁰⁶ Moyo Wake unafanana ndi anthu onse. Chinamkomera Mulungu kumukantha Iye. Ndipo, tsopano, chifukwa chiani Iye anamukantha Iye? Kwa chifukwa chomwecho Iye anasowa kumukantha Adamu.

¹⁰⁷ Tsopano ife tikumuona Iye wokhomedwa, wokanthidwa wa Mulungu ndi wosautsidwa, Mwanawankhosa wangwiro kwa wochimwa—wophedwera ochimwa, Mbambande yangwiro.

¹⁰⁸ Tsopano, kwa pafupi zaka zikwi ziwiri, Mulungu wakhalanso akumpangira Iye Mbambande. Chifukwa, Iye anamukantha Adamu kuti akatenge mba-...chidutswa cha iye, gawo la iye, nthiti kuti ampangire iye mkazi. Ndipo tsopano Mbambande yangwiro imene Iye anayikantha pa Gologotha, Iye anatenga chidutswa kuchokera kwa Iye. Icho changokhala Chipangano Chatsopano, ndicho chonse. Iye anakwaniritisa Chipangano Chakale. Tsopano ndi Chipangano Chatsopano, chidutswa china choti chikwaniritsidwe. Onani, Chatsopano ndi Chakale ziri mwamuna ndi mkazi. Mukuona? Ndipo izo zinatengera Chatsopano kuti chiwo-... Chakale kuti chiwonetseretu Chatsopano; Khristu kubwera, Mbambande, kuti akwaniritse icho. Tsopano Mkwatibwi Wake adzakwaniritisa chirichonse chimene chiri mu Chipangano Chatsopano. Mbambande ina ili mkupangidwa.

¹⁰⁹ Monga zinamutengera Iye zaka zikwi zinai kuti apange Mbambande iyi; tsopano Iye wakhala, kwa pafupi zaka zikwi ziwiri akupanga Mbambande yina, Mkwatibwi wa Khristu, Mbambande yina. Mu kuchita chotero izo, Iye akupanga

izo mwa njira Yake yosasintha konse, njira yomweyo imene Iye anapangira Mbambande; Mawu Ake. Ndiyo njira imene Iye amapangira Mbambande Zake, chifukwa Iye angakhale Mbambande yangwiwo chabe pamene Iwo ali Mawu angwiwo.

Dothi lirilonse, chonyansa, zoyikidwamo, izo zidasweka. “Koma miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu awo sadzasweka konse. Inu mukumbukira, mu kudula daimondi, kuti inu muyenera kukhala ndi chida changwiwo kuti muchitire nacho izo, osati kungoti chidutswa chirichonse chichita izo. Ine ndaona matani a zoperera zazikuluzo zikuperesedwa kupyola pomwepo, ndi kuwasunthira matani akuluwo pamwambapo, kumupsyinja daimondi kupyola pa ameneyo. Ai, izo sizimaswa daimondi. Iye ayenera kudulidwa.

¹¹⁰ Tsopano Iye akuchita chinthu chomwecho mwa njira Yake yosasintha. Ife tikupeza, mu Malaki 3, Iye anati, “Ine ndine Mulungu, ndipo Ine sindisintha ayi.” Iye sangasinthe kachitidwe Kake.

¹¹¹ Tsopano, monga Iye anayamba mwa Abrahamu. Kutachitika kugwa kwa mbambande yoyamba, Iye anayamba mwa Abrahamu, pa maziko, kuti amange mbambande yina.

Iye anayamba pa Tsiku la Pentekosite, kumanga Mbambande yina, Mbewu yapachiyambi, Mawu. Inayamba mu Mpingo woyamba. Chinali chiani icho? Mbewu, Mawu, Mawu kuwonetseredwa, lonjezo limene linali litaperekedwa. Yoweli anati, “Kudzachitika m’masiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse; ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera, akulu anu adzalota maloto, anyamata anu adzaona masomphenya.” Chimene Iye amati adzachite m’masiku otsiriza, awiri, zaka zikwi ziwiri zotsiriza.

¹¹² Zindikirani, ndipo icho chinayambika ngati chapachiyambi. Monga Yesu ananena, “Mawu a Mulungu ndiyo Mbewu imene wofesa anafetsa.” Ndipo Iye anali Wofesa. Mbewu inali Mawu. Ndipo, zindikirani, mbewu iliyonse imene ikhala yokha siimachita kanthu. Iyo iyenera kugwa mu nthaka kuti ibweretse mphukira zakenso. Ndipo Mbewu iyi, Mpingo wangwiwo uwo, unagwera mu nthaka ku Nicaea, Roma, pamene iwo unakhala chipembedzo.

¹¹³ Tsopano, azambiriyakale, kumbukirani. Ndipo inu amene muti mudzamvere tepi iyi, muyifufuze iyo ndi kupeza ngati izo siziri zolondola. Mpingo unafa ku Nicaea, Roma, pamene iwo unatenga nthano ndi zikhulupiro, m’malo mwa Mawu apachiyambi. Chinali chiani icho? Mulungu anali atawonetsera, mwa Mpingo woyamba uwo, kuti Iye anali Mulungu. Iye anali ndi Mpingo utapangidwa kukhala wangwiwo; koma Mpingo, monga mbewu zina zonse, uyenera kugwera mu nthaka ndi kufa. Tsopano, iyo inagwera mu nthaka, ndi kufa, ndi kutaika chotero.

¹¹⁴ Inu mukudziwa, ine ndinawerenga bukhu, kuno osati kale kwambiri. Wina wake analemba bu—bukhu, ndipo anati, *Mulungu Wachete*. Inu mukhoza kuti munaliwerengapo ilo. Ine ndaiwala, ine—ine ndikuganiza Brumback... Ai, ine sindiri, ine sindikutsimikiza ndani amene analilemba ilo. Koma ine sindingathe kukumbukira. Ine ndinali nalo ilo mowerengera mwanga. *Mulungu Wachete*, anati, “Mulungu, kupyola mu zaka zikwi za mibadwo ya mdima, anakhala duu ndipo sanagwedeze dzanja kuse, ndipo anayang’ana anthu ofera okhulupirika akupita ku mbuna za mikango; ndi kuotchedwa ndi Aroma; maphedwe a mtundu wonse; akazi kuvulidwa zovala zawo, kuyatsa moto kwa tsitsi lawo lalitali, ndi phula, nawatentha iwo.” Kumbukirani, tsitsi lalifupi poyamba linayambira mu Roma. Ndipo akazi Achikhristu anali ndi tsitsi lalitali, kotero iwo—iwo amalinyika ilo mu phula nawayatsa iwo moto, ndi kuwatentha iwo, ndipo iwo ali maliseche; nawadyetsa iwo kwa mikango. Ndipo wolembe ameneyo akupitirira kuti, “Alikuti Mulungu ameneyo?”

O, khungu la munthu, nthawizina! Kodi inu simukudziwa kuti Mbewu iyo inayenera kufa? Iye sanayerekeze kuwawombola iwo. Iwo anapita pansu mu chigonjetso. Iwo anapita pansu, akuchucha magazi ndi kufa, kupereka miyoyo yao. Chifukwa? Iyo inali Mbewu. Iyo inayenera kugwera mu nthaka, monga, I, Yohane 12 amatiuza ife. “Mbewu ya tirigu, iyenera kugwera mu nthaka ndipo m’menemo kufa; ndipo osati kufa kokha, koma kuwola.” Koma chipembedzo icho chinadziwa mochepea kuti Moyo uwo unali momwemobe. Ngakhale mpingo mwa iwo wokha... .

¹¹⁵ Ku Nicaea Khonsolo iyo, ya masiku khumi ndi asanu a msutsano wa andale zauthakati, pamene olemerawo anabwera m’menemo nafuna kulowetsa anthu olemekazeka awa mu mpingo. Ndipo aneneri anabwera kuchokera mu chipululu icho uko, akudya zakuthengo ndipo atavala zikopa za nyama, aneneri enieni, ndipo anawaponya iwo kunjja. Chifukwa? Mbewu iyenera kugwera mu nthaka. Iyo iyenera kufa.

¹¹⁶ Iyo inafa mu mibadwo ya m’dima, pansu mkati mwa mdima wa dothi. Iwo anaganiza iyo inali itatheratu. Inu mukudziwa, Yohane Woyera 12:24, Yesu anati, “Kupatula njere ya tirigu ikagwera mu nthaka, iyo ikhala yokha.” Ndipo Mpingo woyamba unali mphukira iyo, Mkwatibwi uyo, Mbewu iyo, Mawu awo anapangidwa kuwonetseredwa, omwe anagwa mu nthaka ku Nicaea, Roma. [M’bale Branham akugogoda pa guwa kochulukana—Mkonzi.]

¹¹⁷ Mverani, Mpingo, ku mafuko onse amene ati adzamve ichi. Apo pali dothi lanu, ndilo zipembedzo zimenezo. Kumeneko ndi kumene Mawu anapachikidwa, ndipo iwo anavomereza nthano. Ndipo kwa zaka mazana mazana mibadwo ya mdima, Mphamvu ndi kuwonetsedwera kwa Mawu kunabisika kwa

dziko. Chikatolika chokha chinkalamulira. Ife tonse tikudziwa zimenezo, monga powerenga mbiriyakale. Chikatolika chokha chinkalamulira.

¹¹⁸ Koma, inu—inu simungabise Mbewu yophuka, Iyo iyenera kutulukira chifukwa (motani?) Wosema wamkulu ali pa ntchito. Iye amanga kachiwiri. Kotero Iye. . .

Mbewu inapita pansu, Mawu.

¹¹⁹ Pamene ife tikuona Paulo Woyera, Petro, Yakobo, Yohane, onse awo amene analemba Mawu. Ndipo iwo analemba, Mawu amene iwo analemba anakhala amoyo, nakhala moyo, ndipo Iwo anakhala moyo. Ndipo pamene ife tikupeza, iwo atatha kuyamba kukhwima, Yohane akuyamba kulemba mu makalata, iye anaponyedwa pa Chisumbu cha Patmo atamuwotcha kaye mu mafuta kwa maora makumi awiri ndi anayi. Koma Mawu ayenera kutulukira. Iwo ayenera kulembedwa. Iwo sakanakhoza kuphika Mzimu Woyera uchoke mwa iye, ndi mafuta, kotero iye anatulukira. Ntchito yake inali isanathe. Iye anafa imfa yachirengedwe.

¹²⁰ Polekapu, amene anali wophunzira wa Yohane, anapitiriza Mawu mtsogolo. Ndipo kuchokera pa Polekapu kunadza Ireniyasi. Ndipo Ireniyasi, munthu wopambana wa Mulungu amene anakhulupirira Uthenga womwewo umene ife tikuwukhulupirira, “Mawu ali olondola.” Mpingo kuyesera kuwufinyira Iwo kunjira.

¹²¹ Potsiriza iwo unafika ku Nicaea, Roma, ndipo kumeneko iwo unagwera mu nthaka, pambuyo pa Marteni Woyera, ndipo anaphedwa. Marteni Woyera anakhulupirira chinthu chomwechi ife tikuchikhulupirira. Iye anaima pa chinthu chomwechi; ubatizo wa Mzimu Woyera, ubatizo wa m’madzi mu Dzina la Yesu. Iye anayima mu chinthu chomwechi chimene ife tikuchita. Ndipo iye anali m’nereri, ndipo anakhulupirira Mawu athunthu a Mulungu. Ndipo potsiriza iwo anapachikidwa, napekesedwa mu nthaka, ndipo anakhala m’menemo kwa zaka mazana, mpaka iwo unavunda chakunja, Mbewu. Matupi okalamba awo avunda. Ine ndafikamo mu Angelo Woyera, mu mphanga, ndi kuwona kumene iwo anafera, ndi mafupa awo othyoka ndi zirizonse. Iwo potsiriza anavunda mpaka mafupa awo anaonongeka, koma Moyo unali udakali pamenepe.

¹²² Njere ya tirigu imene inagwera mu nthaka pa . . . ku Nicaea Khonsolo, inayamba kuphukanso, mwa Marteni Lutera. Monga njere iliyonse ikamamera, kapena tirigu; mbewu zitawola kaye, moyo unaphukira. Ndipo iyo inayamba kuphuka mwa Marteni Lutera. Anachita chiyani iye, chinthu choyamba? Kukana chipembedzo cha Chikatolika, kutsutsa kuti icho chinali cholakwika. Pakuti, iye anati, “Olungama adzakhala moyo mwa chikhulupiriro.” Chinali chiani icho? Kamoyo kofooka kakang’ono kamene kanatulutsa timasamba tiwiri. Amenewo

anali a Lutera. Iyo zedi siimawoneka ngati njere imene inapita mu nthaka, koma Moyo ukubwera kunja tsopano.

¹²³ Ndiye iyo inapitirira ku phesi. Ndiye chinachitika ndi chiani? Mu masiku a Joni Wesile, anachita chiani iye pamene anabweretsa kuyeretsewa? Iye anayima nawo Mawu. Ndipo iwo anachita chiani? Alutera anapatuka ndipo anapanga bungwe, kotero iyo inali nthawi yoti chinachake chichitike. Mbambande ikumangidwa tsopano. Iye anachita chiani? Iye anachita chiani? Iye anatsutsa mpingo wa Anglicani, anatulukuka mu kukonzanso ngati ngayaye. Ndi chiani ichi? Mbewu ikudza ku Moyo, ukumera tsopano.

¹²⁴ Tsopano, phesi silikuwoneka ngati mbewu, ngakhalenso ngayaye.

¹²⁵ Tsopano, abale Achipentekosite ku mafuko onse, ine ndikufuna inu mumvetse, m'bale wanga. Ngati uno uli Uthenga wotsiriza woti ine ndilalikire, Iyi ndi mbambande yanga. Kodi inu mukuzindikira pamene tirigu. . .mbewu ya tirigu imene igwera mu nthaka, pamene iyo iyamba kubwereranso ku yake—mbewu yake kachiwiri?

¹²⁶ Yang'anani chirengedwe. Chirengedwe chimodzimidzi, chiri Mulungu. Mulungu kugwira ntchito mu chirengedwe, ndi zonse zomwe Iye angachite. Koma kuchokera ku chitsitsimutso cha Pentekosite, monga iwo amaganizira, inali Mbewu; iyo siinali. Tsopano penyani. Koma chinachake chinatulukira chofanana basi ngati Mbewu. Tsopano penyani chimene Yesu ananena, mu Mateyu Woyera 24:24, kuti, "Mizimu iwiri mu masiku otsiriza idzakhala yoyandikana kwambiri limodzi kuti iyo ikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka."

¹²⁷ Tsopano, phesi ilo siliwoneka kanthu ngati mbewu; ngakhalenso ngayaye siimawoneka ngati mbewu. Koma zindikirani tsopano, osati mu tsiku la Lutera, koma mu tsiku lotsiriza.

¹²⁸ Chinthu choyamba. Pali alimi a tirigu akhala muno. Chinthu choyamba chimene chimatulukira pa mbewu ya tirigu, inu mukhoza pafupifupi kuganizira kuti iyo inali mbewu, koma (ndi chiani icho?) iwo ndi mankhusu. Iwo amapanga kanthu kakang'ono kakunja, monga, kuti chigwire mbewu. Icho chimapanga mankhusu. Koma mankhusu sindiwo mbewu, mosaposa chomwe ngayaye kapena phesi zinali. Iwo ndiwo modzera moyo chabe, njere ya tirigu, kotero. Yohane Woyera 12, inu mukuona, Yesu akulankhula.

¹²⁹ Tirigu, pambuyo pa ngayaye (pambuyo pa Wesile), amayamba mankhusu, amene ali ofanana kwambiri ndi mbewu ya chinthu china chirichonse. Mankhusu akuoneka kwambiri ngati njere. Iwo akufika pofanana kwambiri ngati njere nthawi zonse, imene inapita mu nthaka. Ndipo pamene ilo

lituluka, phesi, ilo limakhala ndi Moyo mwa ilo, koma zedi siyiri njere. Zimatuluka ngayaye, ufa, komabe iwo siuli njere. Ndiyeno amabwerapo mankhusu, ndipo iwo amangokhala mu mawonekedwe a tirigu, kungokhala chimodzimidzi ngati njere ya tirigu, komabe siali tirigu. Kungokhala chimodzimidzi mu mawonekedwe omwewo, mwangwiro.

¹³⁰ Achipentekoste anatuluka chimodzimidzi ngati m'mene tirigu akanatero. Chirichonse chimatuluka mwa chinzake, kutuluka mwa chinzake, koma izo zangokhala zonyamulira. Iwo amapita ku dinomineshoni. Ndipo ndizo zimene Pentekosite inachita, inapita ku dinomineshoni. Ndipo Pentekosite inachita chiani pamene iyo inatuluka ngati njere? Iyo inabwereranso, monga mu Chivumbulutso 17, kwa m'modzi wa zipembedzo zapachibale. Ndicho chimodzimidzi chomwe chiri. Ndizo zimene Yesu ananena.

¹³¹ Tsopano penyani. Uthenga utulukira kupyolera mwa Lutera, kupyolera mwa Wesile, kulowa mu Pentekosite, ndipo pa masiku otsiriza iwo adzanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheka. Osankhidwa! O, abale Achipentekosite, kodi inu simungawone?

¹³² Tirigu mu chiyambi chake choyamba amangokhala ngati mbewu, pamene iye ayamba kupanga ngati mbewu, koma ndi mankhusu. Iwo anapanga chipembedzo, anachita chimodzimidzi chinthu chomwecho iwo anachita mmusi muno mwa Lutera. Mu Chivumbulutso 17, apo akutsimikizira chinthu chomwecho, cha mipingo.

¹³³ Tsopano, njere ya Mbewu, pachiyambi, inagwa ku Nicaea, pakuti chinali chipembedzo choyamba.

¹³⁴ Zindikirani apa, Moyo umene unali mu phesi, ngayaye, wonse tsopano ukutsirizira mu Mbewu. Moyo umene unatuluka mu Mbewu yapachiyambi, unadza kupyolera mu njira zosiyana, (njira zitatu zosiyana), ndiyeno kubwereranso mpaka ku chikhalidwe Chake chapachiyambi. Aleluya! O, mai! Ndine munthu wosangalala koposa mu dziko, kuti Mulungu wandilola ine kuchiwona Ichi. Penyani momwe Mawu aliri angwiro ndi izi (chirengedwe) zimagwirira ntchito palimodzi.

¹³⁵ Monga ngati momwe ife timatsimikizira chiwukitsiro; kutuluka, dzuwa; kulowa kwa dzuwa; kutulukanso.

Tsamba kuchoka pa mtengo, pansu mkati, utomoni kulowa mu mtsitsi; nubweranso mmwamba, ndipo—ndipo tsamba limabwereranso mmwamba palimodzi nawo. Ilo limagwa pa nthaka; moyo wa mtengo umayamwa iwo kubwereranso, kashiamu ndi potashi, ndi kuubweretsanso ku tsamba lina kachiwiri.

Mukuona, chirengedwe chonse, chirichonse chimagwira ntchito palimodzi ndi—ndi Mawu a Mulungu. Ndipo apa ndi izi, chimodzimidzi, mwangwiro mu Mibadwo iyi ya Mpingo. Ndicho chifukwa chake Mzimu Woyera unatsika nujambula

zinthu zimenezo, nutipangira ife izo m'mene Iye anachitira. Ndizo chimodzimodzi.

¹³⁶ Zindikirani, apa, Moyo umene unali mu nkhusu. Mu phesi, ndi mu ngayaye, mu mankhusu, wonse umasonkhana mu Mbewu. Ndipo Moyo umene unali mu phesi, unapita, umodzi unapita kukapanga unzake. Kulungamitsa, kunakonza njira ya kuyeretsa; kuyeretsa, kunakonza njira ya ubatizo wa Mzimu Woyera; ubatizo wa Mzimu Woyera, unakonza njira ya Mzimu Woyera Iyemwini kuti adze pansi pomwe mwa ungwiro, kubwerera ku Mawu kachiwiri, ndi kudzadzikwaniritsa Iyemwini.

¹³⁷ Koma, chimene chinapanga chipembedzo, chimafa. Monga Moyo, mwa Lutera, unapitirira kukapanga Wesile; ndipo—ndipo, kuchokera mwa Wesile, Iwo unapita ku Pentekosite; ndipo, kuchokera ku Pentekosite, kukapanga Mbewu yapachiyambi. Mpaka ku Pentekosite, anatuluka kuchokera mwa Wesile, mpaka nthawi imeneyo. Chifukwa chomwe Pentekosite anatuluka mwa Wesile, chifukwa iwo sanali chipembedzo, Pentekosite anali. Ndiye Pentekosite inalowa m'chipembedzo, ndipo (anachita chiani?) anasandulika mankhusu. Icho chinkawoneka ngati Chinthu chenicheni.

¹³⁸ Ndipo, aliyense, ndi angati amene anaonapo mbewu—mbewu ya tirigu ikuyamba kumera? Choyamba chaching'ono n'chiani? Ndi chofanana kwenikweni ngati mbewu, koma iwo ndi mankhusu.

Mukuona masiteji atatuwo? Phesi; ngayaye, kapena ufa; ndiye mankhusu; ndiyeno, kuchokera mu mankhusu, mumatuluka Mbewu ya pachiyambi. Mukuona? Osati Mbewu; iwo unali Moyo wa Mbewu, ukukula kupyolera mu ichi, kufika pokhala Mbewu. Amen, amen! Kodi inu mukuchiwona icho? Ndi chiani ichi? Chiwukitsiro, kubwerera ku Mbambande kachiwiri, monga Imodzi imene inabzalidwa.

¹³⁹ Pentekosite anatuluka kuchokera mwa Wesile, chifukwa Wesile anali bungwe. Pentekosite inatuluka, osati ngati bungwe, ndiyeno anasandulika lina. Iwo anayenera kutero, kuti apange mankhusu. Mawu owona a Moyo pa iwo, anali panjira yake ndiye yokakhala Mbewu yapachiyambi, kupyolera m'masiteji awa. Kupyolera mu phesi, ndiye kufika mu ufa; kuchokera pa ufa, kufika pa mankhusu; ndipo kuchokera ku mankhusu, Iwo anapanga Mbewu.

¹⁴⁰ Ayi, phesi, ngayaye, mankhusu, amoyo, iwo anabereka (mu chitsitsimutso chawo choyambirira) chotengeramo cha gawo lina la Moyo wa Mbewu; koma, pamene iwo anapanga bungwe, Moyo unatuluka kuchokera umo. Icho chikutsimikiziridwa ndi mbiriyakale yonse. Palibe bungwe linachitapo chinthu ilo litasandulika bungwe. Ilo linali lakufa. Izo nzolondola.

¹⁴¹ Penyani, Moyo ukuyenda mopitirira tsopano. Iwo ukusuntha patsogolo.

¹⁴² Zindikirani, chimene iwo achita, ena onsewa achita, zatsimikiziridwa ndi mbiriyakale chimodzimodzi basi momwe mpingo wayendera, osati nkudzakhalanso ndi ntchito kwa Iye. Bungwe laikidwa pa alumali. Sipanakhale konse, mu mbiriyakale yonse, mpingo, iwo utatha kukhala bungwe, koma chomwe iwo unafa. Ndipo bungwe limafa ndipo silinadzukenso. Kodi inu simungachiwone icho? Anthu amene ali akhungu, tsegulani maso anu! Chirengedwe ndi Mawu kugwirizana palimodzi ndi kutsimikizira pomwe pano kuti Ichi ndi Choonadi, kuti Icho ndi Choonadi. Moyo uwo umachoka mu phesi, kukapanga ngayaye; kuchokera ku ngayaye, Iwo umapanga mankhusu; ndipo kuchokera ku mankhusu, Iwo umapita Kuchiyambi kachiwiri. Zindikirani, wosati nkudzakhalanso ndi ntchito kwa Iye.

¹⁴³ Kuzindikirika kwake momwe moyo uwu uli, m'mayendedwe ake mu njere ya tirigu, kusiyana ndi momwe uliri mu mtengo. Mulungu anawatcha anthu Ake ngati mtengo; mukuona, moyo umatsika, mu mtengo, ndi kubwereranso mmwamba; umapita pansu ndi kubwereranso mmwamba; mwaona, iwo umapita pansu ndi kubweranso mmwamba. Koma, mu mbewu ya tirigu, iwo umapita mmwamba kuchokera mu phesi lapachiyambi. . . kupyolera mu phesi, ngayaye, ndi mankhusu; ndipo chinthu chimene iwo unapyolamo, chimafa, kotero iwo sungakhoze kudzeramo kachiwiri. Ndi chiyani icho? Chiribenso ntchito konse. Iwo umapitirira ku ungiro wake.

Ameni! Kodi inu simukuwona chifukwa chake Iye sanagwiritse ntchito bungwe? Iye sangabwereranso mu ilo. Ilo lafa. Koma Moyo umapitirira mtsogolo, kuchokera ku chimodzi kupita ku chinzake. Mukuona, iwo amaika zikhulupiro, ndi kulowetsamo. “Yense amene ati adzawonjezere liwu limodzi, kapena kuchotsamo Liwu limodzi,” mukuona, iye watsekerezedwa ku Moyo. Iyo iyenera kukhala Mbewu Yamoyo ikupita mtsogolo.

¹⁴⁴ Ine ndikugwiritsa ichi mu fanizo tsopano, la Mkwatibwi, Mbambande imene ikutulukira. Pamene Mbambande inagwa, apo pali Mbambande ikutulukira. Mbambande inagwa pa Pente- . . . ku Nicaea, Roma, ku Nicaea. Pambuyo pa Nicaea, Roma, Iye akudza podutsa mzochitika, koma Iye akubwereranso mmbuyo kwa Mbambande ija, yopangidwa yangwiro, chifukwa Iye ali gawo la Mawu awo amene analankhulidwa ndi Iye. Iye adzakhala ndi “Mpingo wopanda banga kapena khwinya.” Iwo sudzalumikizidwa mulimonse ndi bungwe lililonse kapena chipembedzo, chinthu chotembereredwa. Iwo wayola mu zinthu zimenezo, koma iwo sudzakhala kumeneko.

¹⁴⁵ Zindikirani, mbewu ikubwera mmwamba, Moyo uwo ukubwera mmwamba, osati kubwerera mmbuyo. Sikudzakhalanso chiwukitsiro china chitatha ichi. Moyo ukubwera mmwamba, kupita ku ungwiro wake, chiwukitsiro.

Zindikirani, mankhusu anatulutsa—m...Zindikirani, mankhusu amatulutsa kunja Mbewu yapachiyambi mwa iyo yokha. Mu Chivumbulutso, mutu 3, ife tikupeza izi.

¹⁴⁶ Tsopano kumbukirani, palibe mpingo wina uliwonse womwe Iye anayikidwa kunja kwake, mu Baibulo, wa Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo. Ndi angati amene akukumbukira izi? Iye anapyola mu M'badwo wa Mpingo, kupitirira kuti apange chinachake. Koma, uno ndi Iwo. Palibenso chinthu china. Koma wo—Wosema wabwerera ku ungwiro kachiwiri, Mawu. Mukuona? Musabwerere mmbuyo. Nzosiya chotani Izo. Inde. O!

¹⁴⁷ Ndipo zindikirani ndiye, mankhusu, pamene iwo atulukira, amangowoneka ngati Njere. Koma pamene Moyo wa Njere uyamba kusiya mankhusu, kuti upite kukapanga Njere (Mkwatibwi), mankhusu amatseguka ndikuyitulutsa Njere kunja. Kodi izo nzolondola? Chirengedwe, ndizo chimodzimodzi zomwe iye anachita.

¹⁴⁸ Mu—mu Chivumbulutso 3, ife tikupeza M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya ukumutulutsa Iye kunja. Tsopano, onani, izo sizinatero, mmbuyo mu mibadwo inayo, chifukwa panali chinachake choti chikapangidwebe. Iwo unangopyolamo ndi kupita ku unzake. Ine ndakuwuzani inu, nthawi yonse, kulibenso chipembedzo china chikudza. Ife tiri pa mapeto. Ndipo iwo anamuyika Iye kunja chifukwa (chiani?) Iye—Iye—Iye ndi Mawu, kachiwiri. Iye ali ngati Awo amene anagwa Pansi apo. Iye ndi Chiphunzitso chomwecho chimene chinatulukira kuchokera pachiyambi.

¹⁴⁹ Ndipo pamene Mbewu ya Mawu iyamba kukula, mankhusu amatulutsa Iyo kuchokera mwa iwo eni. Moyo umasiya zina zonsezo, kuti utsate Iyo. Ndiwo okhulupirira owona, iwo amawutsata Moyo kulikonse kumene Moyo upita.

¹⁵⁰ Monga mu Israeli, choyimira changwiro, ngati ife tikanakhala nayo nthawi; ndangotsala ndi maminiti ochepa. Koma mwa choyimira changwiro, poyamba, kulikonse kumene Lawi la Moto lija linapita kunali Moyo. Mulungu anali Kuwala kumeneko. Ndipo ine sindisamala kaya panali pakati pa usiku, kapena kaya iwo anali pa malo osankhidwa abwino; pamene Lawi la Moto ilo linasuntha, lipenga linalira ndipo Israeli ankasuntha nalo Ilo.

Aleluya! Ndipo pamene lipenga linalira, Marteni Lutera anatuluka kunja ndi Ilo. Ndipo iye anapanga bungwe, kupha... osati iye mwini; mwamuna pambuyo pa iye. Ndiyeno Mulungu

anawuchotsa Moyo mwa ilo, naupitiriza Iwo, nauika iwo pansu m'manda.

¹⁵¹ Ndiye kunadza Wesile. Iye anawona bungwe lalikululo ilo, kotero iye anawomba lipenga, la kuyeretsewa, Mawu ochuluka. Mukuona? Pamene iye anatero, iwo anasunthira kunja, kunja komwe kwa—kunjia komwe kwa Lutera, mpaka mu Methodisti.

¹⁵² Ndipo pamene Pentekosite inawona Ilo, iwo anawomba—lipenga, ndi nthawi ya kubwerera kwa m'phatso. Mukuona chimene iwo anachita? Iwo anawomba lipenga, ndipo iwo anatulukira. Ndiye iwo anapanga bungwe.

Koma, kumbukirani, pambuyo pa mankhusu, ndiwo masiteji atatu amene ife tikuwadziwa, palibenso china chatsalira koma Njere. O Mulungu! Ndiyeno Njere ikutulutsidwa kunjia kwa izo zonse. Amenii ndi amenii! Mbewu Mawu ayamba kudzipanga Okha, Moyo ukutulutsidwa kunjia kwa . . . Tsopano zindikirani, ngatii Mkwatii, chiyambi, woyamba, Mkwatii . . . Uyu ndi Mkwatibwi akutulukira.

¹⁵³ Kumbukirani, Mpingo unayamba pa Pentekosite, ndipo Iwo unagwa ku Nicaea. Iwo unayamba kuphuka, osatii ngatii Mbewu yeniyeni, ai; iwo unalii wina wa Moyo m'menemo, koma iwo unaphuka polinga kuti ukapange bungwe. Ndipo Iye anapyola mu bungwe limenelo. Ndiyeno Iwo unachita chiani? Ndiye Iwo unapita, kuchokera mu bungwe limenelo, Iwo unapita mu bungwe lina, unapita mu siteji ina ya Mawu; kulungamitsa, kuyeretsa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Mukuona? Ndipo pamene Iwo unapyola mu phesii ilo ndi dongosolo, Iwo unapitirirabe kudza mochuluka.

¹⁵⁴ Kumbukirani, ufa mochepe uli mochuluka, ngayaye ilii mochuluka ngatii Mbewu koposa momwe phesii lilirii. Ndipo mankhusu alii mochuluka ngatii Mbewu koposa momwe ngayaye inalirii. Koma Mbewu Iyoyokha ndi yopitirira pamenepo. Mukuona? Iyo inangowiritsa ntchito izo monga mtengatenga, kuti idzitengere Iyoyokha kupyolamo.

¹⁵⁵ Zindikirani, Mkwatibwi. Ngatii Mkwatibwi, pachiyambi, analii Mawu, kapena Mkwatii; ndiyeno ngatii Mkwatibwi watengedwa kuchokera mwa Mkwatii, Iye ayeneranso kukhala Mawu. Zindikirani, Mkwatibwi ayenera kukhala.

¹⁵⁶ Chifukwa, chifukwa chiani Mkwatii ayenera kukhala Mawu okwaniritsika, owonekera poyera? Ndi chifukwa Mkwatibwi ndi Mkwatii alii Amodzi. Iye wangokhala gawo lokanthidwa kuchokera mwa Iye. Apo pali Mbambande. Iyo inakanthidwa.

¹⁵⁷ Michelangelo Woyera sakanakhoza kuyipanganso iyo. Iye sakanakhoza kuyibwezeretsanso iyo.

Koma Mulungu achita izo. Iye adzamubweretsa Mkwatibwi wamng'ono uyu, wokanthidwayo, kubwerera ku Mawu omwe

apachiyambi. Ndipo ndi Iyo, apo pali Mbambande, banja likubwereranso m'munda wa Edeni.

¹⁵⁸ Mkwatibwi uyu azichita motani izi? Kodi Tirigu uyu azichita motani izi? Malaki 4 anati, mu masiku otsiriza, izo zikanadzabwezeretsedwanso, (chiani?) kubwezeretsedwanso monga poyamba; kuyitengera iyo mmbuyo! "Ine ndidzabwezeretsa," atero Ambuye, "zaka zonse chimbalanga, ndi chirimamine, ndi zinthu zina zonsezi zinadya. Ine ndidzabwezeretsanso." Malaki 4 anati, "Iye adzabwezeretsa mitima ya anthu, ndi Chikhulupiro cha anthu, kubwereranso ku chapachiyambi cha atate." Mukuona? Ife tikuchiona ichi patsogolo pathu pomwe, Mpingo. Kodi ife tiri pati?

¹⁵⁹ Tsopano, kutseka mu mphindi zochepa. Ine ndikufuna inu muzindikire mwatcheru kwenikweni za chinachake chimene chachitika kumene.

Malaki 4 abwezera mmbuyo, kubwerera ku chapachiyambi.

¹⁶⁰ Iye wakanthidwa kuchokera mu mpingo, kuchokera ku thupi la mpingo; wakanthidwa ndi Mbuye wake, pa cholinga chofanana. Iye ali Mawu. Mofanana kumene monga Yosefe anakanthidwa kuchokera kwa abale ake, chifukwa iye anali Mawu. Ndipo Yesu anakanthidwa kuchokera kwa abale Ake, chifukwa Iye anali Mawu. Mpingo wakanthidwa . . . Mkwatibwi wakanthidwa kuchokera ku mpingo, chifukwa Iye ndi Mawu. Apo pali masiteji anu kachiwiri; imodzi, ziwiri, zitatatu, onani, kungokhala chimodzimodzi.

¹⁶¹ Mawu, amoyo ndipo akuchitachita, Mkwatibwi wa Baibulo, osati mkwatibwi wopangidwa ndi anthu; Mkwatibwi wa Baibulo, wakanthidwa ndi wosautsidwa wa Mulungu. "Popanda kukongola kuti ife tikanamukhumbira Mkwatibwiyo, komabe ife tamupenya Iye wakanthidwa ndi wosautsidwa wa Mulungu." Uko nkulondola. Iye akuyima yekha. Mkwatibwi wakanthidwa kuchokera ku zipembedzo zonse, malingana ndi Chivumbulutso 3. Iye wakanthidwira kunja kwa M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya momwe Iye anawukitsidwiramo. Mukuona? Mpingo uwu anawukitsidwa mu M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya; ndiwo mankhusu. Koma ngati awo enawo anapita . . .

¹⁶² Kodi inu anthu Achipentekosite simungachiwone icho, ngati chinacho chinali mankhusu ndipo chinafa? Ngati china icho (phesi) chinayenera kufa, ngati ngayaye inayenera kufa, chotero mankhusu ayenera kufa; masiteji atatu a mabungwe.

¹⁶³ Ndipo kumbukirani, inu munati, "Chabwino, tsopano, panali ngayaye zambiri zikulendewera pamenepo. Pali zochuluka za izi." Eya. Pakhala pali Methodisti, Baptisti, Apresbateria, Alutera, mpingo wa Khristu, zinthu zina zazing'ono zonsezi zimene zinagwera pa icho, masamba ndi zina zirizonse zinalendewera kwa icho, koma chapachiyambi chinali kukonzanso, tsopano, onani.

164 Akuyima yekha, monga Mkwati, “wokanidwa ndi anthu, wonyozedwa ndi kukanidwa ndi mipingo.” Mkwatibwi akuyima motero. Ndi chiani icho? Ndiyo Mbambande Yake, onani, ndiwo Mawu amene Iye angakhoze kugwiritsamo ntchito, kupangidwa kuwonekera. Kukana!

165 Kotero, phesi, ngayaye, ndi mankhusu, sizinakhale konse Mbewu, ayi, koma ziri nthawi zonse kukhala mochuluka monga Mbewu.

166 Tsopano pa nthawi yokolola, Mbewu yabwerera ku Moyo wake wa pachiyambi, kubwerera ku Baibulo. Malaki 4 anati iyo ikanadzabweretsedwa mwa njira imeneyo. O, o, mai! Ziyenera kukhala nazo zonse! Kuti zikhale mwa njira iyi, Izo ziyenera kukhala nawo Mawu onse. Kodi uko nkulondola? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

167 Tsopano kodi Iye ananena chiani, mu Chivumbulutso 10, chimene chikanadzachitika? Chifukwa chiani panali ulendo wa ku Tucson? Kuti atsegule kwa Mpingo. “Mu masiku a mtumiki, a mngelo wachisanu ndi chiwiri, Uthenga wa m’ngelo wa chisanu ndi chiwiri, Mawu onse a Mulungu akanadzakhala atawonetseredwa. Chisindikizo, izo zonse zimene phesi linasiya, za chifukwa chake ndi zonse za Izo, zikanadzapangidwa kuwonetseredwa mu nthawi iyi.”

Kodi izo ndi zimene Mawu ananena? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndiye, ife tikuziwona izo. Ndiye ife tiri pati, onani, kodi ife tiri pati? Pali chinthu chimodzi chokha, kukolola kwafika. Mkwatibwi ali wokhwima mwakufa. Iye ali wokonzekera tsopano Kubwera. Zindikirani.

168 Ayi, icho sichidzakhala konse Ichu. Pa nthawi yokolola, Mbewu yabwerera ku chikhalidwe chake cha pachiyambi, ndipo iyenera kukhala ndi zonse za Mawu, ndi cholinga kuti ikhale Mbewu. Tsopano, inu simungakhale ndi Mbewu ya theka; iyo siyingamere. Mwaona? Iyo iyenera kukhala Mbewu yonse. Iyo iyenera kuti isawonetseredwe...Kunena, “Ine ndikukhulupirira mu ubatizo wa Mzimu Woyera. Aleluya! Ine ndimakhulupirira mu kulankhula m’malirime.” Ilo langokhala gawo la Mbewu, u-nhu, koma tsopano apo zawonjezedwera kwa Izo. Aleluya! Mwaona? Moyo, osati mphatso; Moyo wa mphatsozo. Mukuona, mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ife tiri mu nthawi yotsiriza, abale.

169 Phesi, ngayaye, mankhusu, ziri zakufa ndi zowuma tsopano. Pali chinthu chimodzi chokha chimene chiyenera kuchitika kwa izo, ndicho kusonkhanitsidwa mu Bungwe la Mgwirizano wa Mipingo ya Mdziko kuti zikawotchedwe.

170 Mawu asandulika thupi, chimodzimidzi monga Iye analonjeza mu Luka 17, Malaki 4, ndi onse, mukuona, ndi zolondola, Chivumbulutso.

¹⁷¹ Moyo woona wonse umene unali mu phesi, ngayaye, ndi mankhusu, tsopano ukusonkhana mu Mbewu, kukonzekera chiwukitsiro, kukonzekera kukolola. Alfa wakhala Omega. Ameni. Choyamba kubwera kotsiriza, ndipo chotsiriza chiri choyamba. Mbewu, imene inapita mkati, yadza kupyola mu kuchitika ndi kukhala Mbewu kachiwiri.

Mbewu, imene inagwa m'munda wa Edeni, ndi kufa m'menemo, kubwereranso. Kuchokera mu mbewu yosakhala yangwiro iyo imene inafa kumeneko, kubwereranso ku Mbewu yangwiro, Adamu Wachiwiri.

¹⁷² Eva woyamba amene anagwa, ndipo anagwiritsidwa ntchito mu kukonzanso kwachiwiri. . . kudza kwachiwiri, monga kubala mwana, tsopano wakhala Mkwatibwi woona kachiwiri, Mbewu, kubwereranso kumene ndi Mawu apachiyambi.

Alfa ndi Omega ali ofanana. Iye anati, "Ine ndine Alfa ndi Omega," Iye sanalankhule chirichonse cha pakati. A—ha. "Ine ndine Alfa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza." Inde, bwana.

¹⁷³ Utumiki woyamba ndi utumiki wotsiriza uli wofanana. Uthenga woyamba ndi (wachiwiri) Uthenga wotsiriza uli chinthu chofanana. "Ine ndine, ine ndinali mu Alfa; Ine ndiri mu Omega." "Padzakhala tsiku limene silidzatchedwa usana kapena usiku, koma mu nthawi ya madzulo kudzakhala Kuwala." Mwaona, Alfa ndi Omega, wakhala woyamba ndi wotsiriza. O, mai, abale, ife tikhoza kukhala maora pa izo.

¹⁷⁴ Mbambande zopambana za banja, Adamu Wachiwiri ndi Eva Wachiwiri, tsopano akukonzekera wa ku munda, Zakachikwi, ameni, kubwereranso pa dziko lapansi. Aleluya! Wosema wamkulu sanawasiye iwo kuti agone pamenepo. Iye zinamutengera nthawi, monga Iye anachitira mu zaka mamilioni, kuumba angwiro awiri oyamba; ndipo iwo anagwa. Tsopano zachitika kwa zaka zikwi, Iye waumbanso, ndipo tsopano pano iwo ali okonzeka.

¹⁷⁵ Mbambande yadza ndi kukhudza nthaka; kuchokera ku mbali Yake kwadza womuthandizira.

Ndipo Iye wabweretsedwa mmwamba m'kachitidwe komweko. Tsopano ndi Uyo wabwereranso; ndi chikhalidwe chonse, Baibulo, ndi china chirichonse, kuwonetsera kuti ife tiri pano.

Mitundu ikumwazika, Israeli akuwuka,
Zizindikiro zimene Baibulo linafotokozeratu;
Masiku a amitundu atha, (yang'anani pa
mulu uwu zinthu zopanda ntchito umene
ife tiri nazo), zoopsya zikuchuluka,
Bwererani, O omwazika, kwanu komwe.

Ndiko kulondola. Inu ndibwino muloweretu m'menemo msanga, ngati inu mukupita.

Inu ndikukonzekera kutseka pakangotha maminiti asanu, khumi.

¹⁷⁶ Zindikirani mbambande yopambana, ya banja. Mwamuna ndi mkazi sangakhale banja moona pokhapo iwo atakhala amodzi. Iwo ayenera kuteru. Ngati iwo sali, iwo sali banja labwino; mkazi akukokera mbali ina, ndipo mwamuna kwina. Izo zikanapanga banja lowopsya. Koma mogwirizana, ndi chikondi wina kwa mzake, ndilo banja. Ndipo tsopano iyo inali mbambande ya Mulungu, ndipo tsopano mabanja onse owona pano amawonetsera chimenecho. Mukuona?

Ndipo tsopano banja la Mbambande labweranso, Khristu ndi Mkwatibwi Wake, wakonzeka kudza. Adamu Wachiwiri, Eva Wachiwiri, akonzeka tsopano kubwerera Kwawo. Ndipo chithunzi chonse chakhala chiwombolo. Kuchokera kumene iye anali, kumubweretsa iye mmbuyo, mukuona, chimodzimidzi basi kumubweretsa iye kachiwiri. Atatha . . .

¹⁷⁷ Tsiku lina, nditaima kuno pa Anthu Amalonda Achikhristu. Ambiri a inu, ine ndikuganiza, munali kumeneko. Pamene ine ndinamva kuti wansembe wa Chilutera, kapena mlaliki, kapena anayenera kukhala, atayima pamenepo nalankhula chinthu chopanda pake chija, nanyozetsa chimene ife tikuchikhulupirira. Ndipo iwo Anthu Amalonda a Full Gospel kukhala naye munthu ameneyo pamenepo, nanena zimenezo. Iye anavala kolala yake yotembenezidwira kumbuyo. Ambiri a iwo amavala choncho tsopano. Ndipo iye anati, “Tsopano, anthu amandifunsa ine chifukwa chiani ine ndimatembenezira kumbuyo kolala yanga, anati, ‘Nanga iwo angakusiyanitseni inu chotani ndi wansembe wa Chikatolika.’” Anati, “Palibe kusi yana, ndipo sipayenera kukhala.” Iye anati, “Ife tonse tiri ana a Mulungu.” Iye anati, “Ine ndikudziwa wansembe wa Katolika amene ali wa ponseponse, mukuona, amene akhoza kupezeka paliponse.”

¹⁷⁸ Tsopano inu simungakhale wa ponseponse popanda kukhala wodziwazonse. Mulungu sali ngakhale waponseponse; Mulungu ndi wodziwazonse. Wodziwazonse, chimene chimampangitsa Iye kukhala wa ponseponse, Iye amadziwa zinthu zonse. Koma, kuti akhale Chinthu, Iye anayenera kukhala mwa Chinthu chimodzi. Pokhala wodziwazonse—wodziwazonse, Iye akhoza kukhala wa ponseponse. Chifukwa, Iye amadziwa chinthu chonse, ndipo anadziwiratu izo zisanayambe . . . Iye anadziwa, dziko lisanayambe, utitiri ungate, nsabwe, nkhunguni zingati, ndi kangati kamene izo zidzaphethire maso awo, ndi zina zonse za izo, mukuona, chifukwa Iye ndi wa ponseponse. Inu simungakhale wodziwazonse—wodziwazonse popanda kukhala opandamalire. Ndipo pali chinthu chimodzi chokha chimene chiri chopanda malire; Mulungu. Ameni! Ndipo kenako ife . . .

¹⁷⁹ Ndi chiani icho? Ndi mdierekezi, kuwatengera iwo kumene molunjika kokaphedwa. Aliyense wa iwo kulowamo,

chimodzimidzi momwe Baibulo linanena. Ndipo pano ndi izi, mukuona, kudza pakati pomwe pa Achipentekosite, ndi kungowakoka iwo molunjika monga ngati. . . Ndi nthawi yanji!

¹⁸⁰ O, utatha umboni umenewo, winawake anati kwa ine. . . Ine—Ine. . . Icho chinali chinthu chabwino kuti ine sindinalankhule kwambiri, chifukwa iwo akanandiika ine m'ndende kumeneko. Koma ine ndinangoganiza, “Ndi icho apo.”

A—anthu amene aphunzitsidwa, amadziwa. “Anzeru adzamdziwa Mulungu wawo, m'tsiku limenelo,” izo zinanenedwa mu Daniele. Inde, bwana. Mukuona, “Anzeru adzamdziwa Mulungu wawo.” Iwo akuyang'anitsitsa zinthu zimenezi.

¹⁸¹ Koma pamene ine ndinaona icho chikuchitika, ndipo iwo Achipentekosite atayima pamenepo ndi iye! Ngakhale Oral Roberts anandiyang'ana ine *chotero*. Ine ndinati “O, mai!” Ha! Koma, kuyima pamenepo ndi maphunziro, wopukutidwa, inu mukudziwa, ndi zina zotero.

¹⁸² Iyo si njira imene Mulungu amawapukutira Ake. Iye samawapukuta Ake ndi maphunziro. Iye amawapukuta mwa kudzichepetsa, mu—mu mphamvu ya Mawu Ake okwaniritsika, kuwonetsa mawonekedwe a Mbewu imene Iyo inachokeramo.

¹⁸³ Tsopano, winawake anati kwa ine, anati, “M'bale Branham,” anati, “pali chinthu chimodzi chimene ine sindingachimvetse cha inu.”

Ine ndinati, “Ndi chiani chimenecho?”

¹⁸⁴ Titaima kunja uko mu holo. . . Ine ndikuganiza, Mlongo Dauch ndi iwo, nditatha ine kugwirana chanza ndi Bill, ndipo nditayima pamenepo; ndi onse ndikuzungulira pa kona, ndi gulu lonse la anthu. Mlaliki anadzikanikiza kulowa, kolala itatembenezidwira kumbuyo, iye anati, “Ndi chifukwa chiani iwe nthawizonse umangowakalipira anthu?” Iye anati, “Anthu awo amakukhulupirira iwe kuti ndi wantchito wa Mulungu, wofasa ndi wokoma kwa iwo, ndi chirichonse.” Anati, “Nthawi iliyonse ine ndikumva iwe ukuyimilira, iwe umangowakalipira akazi, chifukwa chokhala ndi tsitsi lalifupi, ndi pa kuvala makabudula, ndi kudzipakapaka, ndi zinthu zina zonsezo; ndipo umawakalipira anthu, ndi kuwafotokozera iwo momwe aliri ozizira ndi ofunda ndi osakonzeka.” Anati, “Chifukwa chiani iwe umachita zimenezo?” Anati, “Anthu amenewo amakukonda iwe. Ungakhale bwanji iwe mwana wachikondi wa Mulungu ndi kumachita chinthu ngati chimenecho?”

Ine ndinaganiza, “Ambuye, ndiloleni ine ndimuyankhe munthu wochenjera uyu. Mukuona? Inu mungondilola ine ndimuyankhe iye, penapake, pamene padzamupachike iye pa chingwe chake chomwe.” Inde.

Ine ndinati, “Chabwino,” Ine ndinati, “bwana, kodi inu munayamba mwawerengapo za wopanga nyimbo wamkulu. . . wopanga nyimbo wamkulu wotchedwa Beethoven.”

Iye anati, “O, zedi, ine ndinawerenga za Beethoven.”

¹⁸⁵ Ine ndinati, “Iye mwina anang’amba mapepala opanda ntchito odzaza dengulu la zinyalala, koma iye anapatsa dziko mbambande.” Iye sanatsegule konse kamwa yake ndikunena liwu lina. Ine ndinati, “Pamene iye ankakhala mu chipinda chake chowerengera pansu pa kudzoza, iye amakhoza kulemba chinthu china apo. Iye amakhoza kupita mowerengera mwake napemphera. Ikapanda kukhala bwino, iye amaying’amba nayiponya mu dengulu la zinyalala. Koma pamene iye anapayola mu kudzedwa konse, dziko linali ndi mbambande.”

O, momwe Mawu amatemera, koma Iwo amapanga mbambande; a-ha, amachotsa mankhulu onse ndi phesi kutaya kutali. Izo zimabweretsa Mbambande.

¹⁸⁶ Ine ndangotsala ndi maminiti asanu ndi awiri kuti ndikufotokozereni inu chinachake chimene chinachitika dzana, kuti tichoke pa nthawi yake. Julaye 3, ine ndinali nditakhala pano mu. . . kokumanira konkuno, malo ogulirako zinthu panja komweku kuno. Ine ndafika mu Pig Alley, ku Roma, ku France, ndipo ine ndafika mu Mzinda wa New York, Los Angeles. Koma gulu la akazi onyansitsitsa amene ndawaona m’moyo mwanga ndi ku Jeffersonville, Indiana. Ine sindinawonapo kuchuluka chotero kwa uve ndi zonyansa m’moyo wanga ngati m’mene ndinawonera pakati pa anthu amenewo. Ine ndinakhala pamene mpaka mtima wanga unandipweteka, ndipo Ambuye anali atandipatsa ine masomphenya.

Tsopano ine ndikufuna kufotokoza masomphenyawo. Ine sindikudziwa ngati ndingawamasulire iwo, koma ine—ine ndifotokoza masomphenyawa kwa nthawi yanga yoyamba.

¹⁸⁷ Ine ndinalowa mu chizimbwizimbwi. Ndipo, pamene ine ndinatero, panali winawake pamodzi nane. Ine sindinamuone munthuyo. Linali Liwu chabe. Ndipo ine—ine ndinayang’ana. Ndipo pamene ine—ine ndinayang’ana mbali iyi, Iye anati, “Mkwatibwi afika powonekera kuti awonetsedweretu.”

Ndipo ine ndinayang’ana, akudza kwa ine, ndipo ine ndinawona koposa—gulu lokongoletsetsa-la akazi ovala mwaukhondo amene ine ndinawawonapo m’moyo wanga. Koma aliyense wa iwo, ankawoneka ngati, anavala mosiyana. Iwo onse anali ndi tsitsi lalitali. Ndipo iwo anali ndi mikono yaitali ndi masiketi, ndi zina zoterozo. Asungwana, iwo amawoneka ngati, ine ndingati, pafupi mwina a makumi awiri.

¹⁸⁸ Tsopano ine ndiri ndi Baibulo lotsegulidwa apa patsogolo pa ine. Mukuona? Ine ndikhoza kungonena chokhacho chimene ine ndinachiwona.

Ngati inu munena, “Kodi inu mukuyang’ana chiani?” Ine ndikuyang’ana wotchi. “Inu mukuyiyang’aniranji?” Ine ndikuyang’anira anthu, kuyang’ana anthu. “Mukuyang’ana chiani?” Ine ndikuyang’ana Baibulo. Ndicho chimene. Ine ndikulankhula Choonadi. Ndicho chimene ine ndikuchiwona. Ndipo ine ndingakhoze kunena chokhacho chimene ine ndinachiwona. Ine sindiku—ine sindikudziwa chimene chiri . . . zonse za icho. Ine ndiyenera kungokufotokozerani inu.

¹⁸⁹ Koma, pamene Mkwatibwi uyu, Iye anali kuyang’ana kumene pa . . . Amene amalankhula kwa ine, ndipo ine, tinayima limodzi. Maso Ake, iye anali wosamalirika, anthu okomakuwayang’ana amene ine ndinawawonapo m’moyo wanga. Kuoneka ngati iwo akanakhala dazeni, kapena kupitirirapo, kungo . . . ine sindikudziwa ndi angati anali patsogolo, koma panangokhala gulu la iwo. Ndipo Iye anadutsa, mokoma, ndi ulemu. Ndipo maso Ake ali m’mwamba, kupenyetsa, pamene Iye anali kudutsa. O, Iye anali wokongola! Ine ndinayang’ana pa Iye, ndipo pamene Iye anali kudutsa. Iye anati, “Tsopano ife tiwonetsanso . . .” Anati, “Uyo ndi Mkwatibwi.

“Tsopano ife tiwonetseratu mipingo.” Ndipo iwo anadza. Ine ndinawazindikira iwo akudzapo. Ndipo pamene iwo anadzapo, aliyense, ankawoneka ngati, ankapitirira kuipa. Ine sindinaonepo gulu lonyansa chotero m’moyo wanga.

Ndipo pamene Iye anati, “Otsatira,” Ine ndinamva phokoso. Ndipo Ilo linati “Otsatira,” anati, “pano pakudza gulu la Amerika.”

¹⁹⁰ Tsopano, ine ndine wa Chimerika, koma ichi—ichi chinangondidwalitsa ine. Ine sindiri wodziwa kulankhula kokwanira, ndiponso, mu chigulu chosakanikirana, kuti ndinene chimene chinali kuchitika. Ine—ine—ine . . . Ndipo inu mudzayenera kuchita kuwera pakati pa mizere. Koma pamene akazi anali kudza, mtsogoleri wao anali mfiti. Iye anali ndi mphuno yaitali kwambiri ndi kamwa yaikulu kwambiri. Ndipo onsewo anali atavala mtundu wa zovala zazifupi zolekeza m’musi umu; koma kumwambaku kunangokhala kalamba, kamene, kakang’ono chabe, kalamba ka pafupi theka la inchi kamene kanadutsa mmwamba anadzikulunga nako *chotere*. Ndipo mkazi aliyense anali ndi chinachake mwa dongosolo . . .

¹⁹¹ Ambiri a inu, zaka zapitazo, inu mumakumbukira pamene ife tinali kudula pepala lija, inu mukudziwa, nyuzipepala, ndi kupanga choyingitsira ntchentche? Ndi angati akukumbukira icho? Inu mukudziwa. Chifukwa, ine ndiganiza kuti iwo amagwiritsa ntchito icho mu maphwando, inu mukudziwa. Kolendewera panso chotero, pepala lochedwa, pepala lolezedwa.

Iwo anali ndi chinthu china chophatika panso pao, *chotere*, chophatika mmusi mwawo. Mbali ina yonse *iyi* inali poyera.

Ndipo aliynse anali ndi tsitsi lodulidwa lalifupi kwenikweni, ndi zinthu zooneka zonyowa monsemo chotero, tsitsi lalifupi kwenikweni-lometedwa; ndipo akhathikhathi ndi zopakapaka. Mtheradi sichina koma amawoneka ngati mahule a mmisewu.

Ndipo iwo anali kuyenda ndi pepala limeneli, ndipo, zonyansa! Tsopano, pepalalo ndicho chimene chimaphimba kutsogolo kwawo. Koma pamene iwo anadutsa pamalo oonetserapo, kumbuyo kwa iwo...Ndipo kuwona m'mene iwo anali kuyendera, kutsogolo kwawo kumene ndi mbali ya kumbuyo kwawo, ndi momwe iwo anali kuchitira!

Ine ndinati, "Kodi umenewo ndi Mpingo?"

¹⁹² Ndipo apo iye anadutsa. Ndipo iwo anali kuyimba nyimbo izi apa za gwedemula ndi sinjonjo, inu mukudziwa, kapena chirichonse chomwe inu mungazitche, akupita mmusi, kuyimba iyo ndi kumapita pamenepo.

Ine ndinati, "Kodi umenewo ndi Mpingo?" Ndipo ine ndinali nditayima pamenepo, ndipo mu mtima mwanga ine ndinali kulira.

Ndipo, mfiti iyi, mwa kulingalira kwanga si chinthu chinanso mu dziko koma iye ali...Iye ali Bungwe lija la Mgwirizano wa Mipingo mu Dziko, kuwatsogolera iwo molunjika kumene kumka mu msewu umene iye anali kupita. Iwo anapita kumbali cha kumanzere, ndipo anazimirira mu chisokonezo; akuyimbabe nyimbo imeneyi namapanga maphokoso oseketsa kwenikweni, ndi kumagwedeza matupi awo, mbali imodzi ndi kenako kumbali inayo. Ndiyeno, motero choncho, kumapitirira monga choncho, akuyenda.

¹⁹³ Ndipo ine ndinangoyamba kuweramitsa mutu wanga, ndipo Iye anati, "Dikira, Mkwatibwi ayenera kubweranso."

Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo apa iwo anabweranso. Ndipo iwo anadutsa pamenepo, madona achichepere owoneka mokoma. Iwo onse anali kuyang'ana kwa ine, pamene iwo anali kudutsa. Ndipo ine ndinazindikira aliynse anavala mosiyana. Ndipo m'modzi wapambuyo akukhala ngati anali ndi tsitsi lalitali likulendewera pansu, ndipo analipiringiza ilo *chotere*; ayenera kukhala m'Jeremani kapena chinachake monga choncho. Ndipo ine ndinawapenyetsa iwo.

Ndiyeno pamene iwo anayamba kuchoka, awiri kapena atatu a iwo, m'mbuyo, anakhala ngati anachoka mu sitepe, ndipo ine ndinawafuulira iwo. Ndipo iwo anali kuyesetsa kubwerera mu sitepe kachiwiri. Ndipo ine ndinawaona iwo, masomphenyawo anangodzimirira chabe nasinthika, kwa ine.

¹⁹⁴ Tsopano pano pali kumasulira kwake pamenepo. Chifukwa... Tsopano, kumbukirani, ine ndinali nditangotsiriza kulemba... ine ndinali ndisanatsirize, ine ndinali

ndisanalembebe zolemba izi. Koma mu kulalikira, m'mawa uno, ine ndinagwira chimene chinali, mu ulaliki wanga womwe. Kodi inu munazindikira, mpingo unangodza powonekera . . .

Tsopano, ndicho Choonadi, amzanga. Atate Akumwamba, Amene amalemba Mawu, akudziwa kuti ine ndikukuwuzani Choonadi. Mukuona? Ine ndikudziwa ine ndikungonena Choonadi.

Ndipo posachizindikira icho mpaka maminiti pang'ono apitawo, zinaoneka ngati, kapena posachedwapa, mwaona. Kodi inu munazindikira? Mkwatibwi anadza poonetsera kawiri; Mbewu yoyamba ndi Mbewu yachiwiri, zonsezo chimodzimidzi ndi Imodzi yomweyo. Ndipo chifukwa iwo anavala—anavekedwa mu zigawo zosiyana, iye adzabwera kuchokera ku mafuko onse, iwo adzapanga Mkwatibwi. Aliyense anali ndi tsitsi lalitali, ndipo analibe zopakapaka, ndipo asungwana okongola kwenikweni. Ndipo iwo anali kundiyang'anitsitsa ine. Icho chinayimira Mkwatibwi kuchokera ku mafuko onse. Mukuona? Iye, aliyense kuyimira fuko, pamene iwo akuguba mwangwiro mu mzere ndi Mawu. Mukuona?

¹⁹⁵ Ndipo, kenako, ine ndinayenera kumuyang'anitsitsa Iye. Iye adzachoka mu sitepe ya Mawu ngati ine sindimuyang'ana, pamene iye akudutsa, ngati iye ati apyolepo. Mwina idzakhala nthawi yanga, pamene ine ndatha, mukuona, pamene ine ndatsiriza, kapena chirichonse chimene chiri.

¹⁹⁶ Chiyani? Iwo anali kubwerera mmbuyo. Kuyesetsa mwakupambana kwao, ndipo anali kubwerera mmbuyo, kungobwerera mu mzere; chifukwa, iwo—iwo anali kuyang'ana kunja kwinkwaka, kuyanganitsitsa za mpingo uja umene umangopita kunja mu chisokonezo. Koma awiri. . . Apatsogolo aja, sanatero. Apambuyo, awiri okha kapena atatu a iwo, anakhala ngati apita kunja pang'ono ku mbali ya dzanja lamanja, ndipo anaoneka ngati akuyesetsa kubwerera mu mzere pamene iwo anali kupitirirabe. Iwo anali kungondipyola ine, o, monga pano ndi pachipupapo, kundidutsa ine. Ndipo ine ndinali kuyima pamenepo. Ndiyeno ine ndinangowawona onse akusunthira kunja ndi kuchoka.

Koma, inu zindikirani, mpingo unangobwera powonekera kamodzi, fuko lililonse, mpingo. Koma Mkwatibwi anabweramo kawiri. Mukuona, mukuona chimene chinali? Tsopano, posachidziwa icho, koma yang'anani pa icho ndi uthenga wanga m'mawa uno. Posachidziwa icho. Mukuona? [M'bale Branham akugogoda pa guwa kochuluka—Mkonzi.]

¹⁹⁷ Mbewu inagwa mu nthaka ku Nicaea. Iyo inali Mbewu yapachiyambi. Ndipo Iye wadza kupyola mu njira ya zipembedzo izi, amene akubwera mkukhalapo kamodzi kokha. Koma Mkwatibwi akubwereranso m'masiku otsiriza. "Ine ndidzabwezeretsa." Mukuona, Mbambande yabwezeretsedwa.

Ndicho chifukwa chake Mkwatibwi anali mu kuwonetseredwa, anawonetseredwa, nthawi yachiwiri. Iye anawonetseredwa koyamba, kenaka anaonetseredwa kachiwiri. Ndipo Iye anali mwangwiwo, nthawi yachiwiri, momwe Iye analiri nthawi yoyamba. O Mulungu, chitani chifundo! Fulumirani, fulumirani, fulumirani, Moyo, lowani mu Mbewu, msanga kumene! A—ha.

¹⁹⁸ Ena onsewo sanaonekenso. Iwo anapita kunja, osabwerera konse kachiwiri.

Koma Mkwatibwi anabwera kachiwiri, chifukwa Iye anali Alfa ndi Omega. Mulungu, Wosema wamkulu, wadzipangira Iye Mbambande, pakuti Iyo ili chiduswa cha Mbambande Yake yoyamba. Yonga Iye anayipanga m'munda wa Edeni, ndipo anatenga chiduswa kuchokerako, ndipo anapanga chiduswa china ndipo icho chinawonongedwa ndipo chinagwa, tsopano Iye wakhalala nthawi yonsezi akuyimanganso iyo. Ndipo Iye anabweretsa Mbambande iyi, ndipo inakanthidwa, ndi cholinga. . . Gawo ilo limene linakanthidwa, linali mwa cholinga kuti ayibweretsenso Mbambande ija, kachiwiri.

¹⁹⁹ Kotero, Mbambande ndi Mwana wa Mulungu, Mbambande ndi Mkwatibwi, ndipo Ili gawo la Iye, limene liyenera kukhala kukwaniritsa kwa Mawu. Mawu akwaniritsidwa, ndipo ife takonzekera Kudza kwa Ambuye.

²⁰⁰ O Mpingo wa Mulungu wamoyo, weramitsani mitima yanu ndipo mwanu—inu nokha pamaso pa Mulungu. Zinthu izi ndi zoonaa. Ine ndikudziwa kuti izi zikumveka chotero, ngati chinthu choposa ngati mmene chidzakhaliremo, chidzafalikira kwambiri ku mafuko. Izo sizinali konse. Iye sasintha njira Yake. Ingokhalani othokoza, Mpingo, khalani othokoza kuti muli pamene muli lero ngati inu muli mwa Khristu. Chifukwa, inu mukuona, tsopano, ndipo pamene icho. . .

²⁰¹ Kumbukirani, Moyo wonsewo udzasonkhanitsidwa mu Mbewu, chifukwa cha chiwukitsiro, koma phesi liyenera kuwotchedwa. Zotsala zonsezo; mankhusu ndi zonse, ziyenera kuwonongedwa, ndipo izo zidzatero. Musadalire mu zanu, zipembedzo izo. Inu mukhale mu Mawu, Moyo, Mulungu ndi Mbambande Yake.

²⁰² Ndiye mu Zakachikwi muli chiani? Khristu ndi Mkwatibwi Wake, kubwereranso m'munda wa Zakachikwi. Amenii!

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvari.

²⁰³ Apo ndi pamene Iye anakanthidwa. “Ife tinamuwona Iye wokhomedwa, wokanthidwa ndi Mulungu, ndi wovutidwa. Koma Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, Iye anatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu yathu.”

204 Kodi pali wina pano, m'mawa uno, amene siali mu Mbewu imeneyo m'mawa uno? Ndipo pamene Moyo tsopano ukukoka gawo lake lotsiriza kuchokera mu mankhusu, popeza mankhusu akuwuma. Ndi angati amene akudziwa kuti mpingo wa Chipentekosite ukuwuma? [Osonkhana, "Ameni."—Mkonzi.] Ndi chiani icho? Moyo ukuchokamo. Monenetsa, iwo wachokamo. Ndipo ngati Mkwatibwi uyo ali kale mu chiwonetsero, ine ndikudabwa ngati Mkwatibwi sanapangidwe kale, ndiye. [M'bale Branham akuyamba kuyimba chong'ung'uza, *Ndim'konda Iye*—Mkonzi].

. . . Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvari.

205 Ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano. Kodi alipo ena pano amene akufuna kukumbukiridwa? Ngati inu mukumverera kuti inu simuli . . .

Amzanga, ndi zomveka kwambiri. Ine sindinakhalepo ndi masomphenya m'moyo wanga, mpakana chinthu china chitachitika, chotsatira. Ine ndimanena Choonadi. Nthawi zina zonsezi, ngati ine ndanena Zooni, Mulungu wazitsimikizira izo. Ndiye, ine ndikunena Zooni nthawi ino.

206 Ine sindikudziwa ndi tsiku lanji limene ife tikukhalamo, koma ine ndikudziwa palibe chinthu chatsalira. Sipangakhale wandale angawuke amene angawongole chinthu chimenechi. Ndale, fuko lapita. O Mulungu! Kodi inu, kodi inu simungazame mwakuya kokwanira ku—ku—kuti mumverere icho. Fuko lapita; osati fuko, koma mafuko. Lino ndi labwino pa gululo, ndipo ilo lapita. Ndiye, ngati mafuko apita, dziko lapita. Ndipo mipingo, mwa kulingalira kwanga, Pentekosite unali wopambana womwe iwo anali nawo, koma iwo wapita.

O Mulungu, tichitireni ife chifundo!

207 Ngati inu simukumudziwa Iye, chonde fulumirani, fulumirani. Ngati inu mukumverera Moyo, chokani apo . . . chokani pa tchimo lanu, chokani mu chinthu chimene inu muli. Fikani ku Mbewu, mofulumira kumene. Inu mudzafera mu phesi, kapena mu mankhusu.

Pempherani, pamene ife tikuyimba tsopano. "Ndimkonda Iye."

Ziri kwa inu tsopano. Ife tiribe chipembedzo, palibe chinthu china. Ife tiri ndi Khristu yekha. Inu muli olandiridwa kudzapembedza ndi Iye, ndi ife, mpaka Iye akadza. Ife sitingalembe dzina lanu pa bukhu; ife tiribe mabuku. Ife tikufuna dzina lanu mu Bukhu la Moyo. Inu mungakhoze kuchichita icho kupyolera mu Kubadwa basi. Kodi inu simuchita icho pakali pano? Mfunseni Khristu Moyo watsopano, akulowetseni inu mkati, alembe dzina lanu pa Bukhu Lake,

ngati ilo mulibe. Ndiye, inu mukhoza kuyanjana ndi ife, ife tidzakonda kukhala nanu. “Ine . . .”

²⁰⁸ Mulungu wokondeka, thandizani munthu aliyense tsopano kuti afufuze, kuwona ngati ife tiri mwa Iye. Inu munatikonda ife. Inu munakanthidwa chifukwa cha ife, ndipo ife tinakupenyani Inu wokanthidwa ndi wosawutsidwa wa Mulungu. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muyitana aliyense. Ambuye, lankhulani kwa ana anga, okonedwa anga, abwenzi anga. Perekani icho, Ambuye, pakali pano, kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu.

²⁰⁹ Musalore winawake adikire nthawi yaitali kwambiri, Ambuye. Zikuwoneka pafupi koopsya. Zokolola zakhwima moona. Zokololera zazikulu za Mulungu zidzasesa kupyola mu dzikoli limodzi la masiku awa, zinyalala zidzawuluka pa njira iliyonse; koma Tirigu adzasonkhanitsidwira ku nkhoekwe, kutengedwera mmwamba, chifukwa mwa Iye muli Moyo. Perekani, Ambuye, chofunsa chirichonse chiyankhidwe, pemphero lililonse kuti liwonekere pamaso Panu.

²¹⁰ Ine ndikuwapempherera iwo, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu musalole aliyense amene ali pano atayike, Ambuye. Iwo—iwo—iwo akukhala movutikira; iwo—iwo—iwo anawongolera mitunda mazana. Ndipo chirichonse chimene ife tikuchisowa, mupereke izo kwa ife, Ambuye, chirichonse chimene chiri chabwino kwa ife, Ambuye; osati chimene chiri chabwino pamaso pathu, koma chimene chiri chabwino pamaso Panu. Ife tikufuna kuyima ngati namwali wangwiro amene walangidwa, wodzudzulidwa ndi Mulungu, kuti ife tikhale oyeretsedwa ku machimo athu. Ndipo ine ndikupereka pemphero langa chifukwa cha iwo, Ambuye.

²¹¹ Ine—ine—ine sindikudziwa momwe ndingapempherere. Ife—ife tikulankhula kwa Mulungu Wamphamvu. Ndipo ndi munthu wanji alipo, wa chivundi uti amene akanakhoza kupanga pemphero loyenera pamaso pa Mulungu wamoyo? Koma, Ambuye, mawu anga osatchulidwa bwino, ndipo anga—ndipo manauni ndi mapulonauni anga mu—m’ malo olakwika; ngati Inu munakhoza kutola ma A B C a mnyamata wamng’ono tsiku lina, ndi—ndi kupanga chiganizo, Inu—Inu mukhoza kunyalanyaza manauni ndi mapulonauni anga ndi kungoyang’ana ku chimene ine ndikukhulupirira, Ambuye.

Ine ndimakhulupirira Inu. Ine ndimakhulupirira Mawu awa. Ndipo ine ndikukhulupirira aliyense pano. Ndipo ine—ine ndikuwabweretsa iwo ku Guwa limenelo, Ambuye, mwa chikhulupiriro, pamene pakati pa ife ndi Yehova Wamkulu pali Mwazi wa Mwana Wake, Yesu. Ndipo Mwaziwo udzatilankhulira ife. Pamene Inu munamukantha Iye pa Kalvari, Inu munati, “Lankhula!” “Mvereni Iye!” “Ndipo Mwazi,” Baibulo linati, “umalankhula zinthu zazikulu kuposa mwazi wa nkhosha mu

Chipangano Chakale, pakuti Mwazi wa Khristu umalankhula zazikulu kuposa mwazi wa Abele; zinthu zazikulu.” Ndipo lankhulani, Ambuye, chiwombolo cha ife, pamene ife tikuyitana kupyolera mu Mwazi.

²¹² Atate Wamkulu wa Moyo, tiyikenimo ife, Ambuye. Ngati ife—ngati ife tachimwa, tichotsereni icho kwa ife. Ife, ife sitikufuna kukhala mwa njira iyo, Ambuye. Icho sichiri cholinga chathu.

Ndipo ife tikuzindikira kuti ife tikukhala mu yoopysa, njira ya mdima. Monga ife tinanena poyamba, ife tikuyenda chokwera phiri, kupyola malo oipa. Mkwakwalala wake wosawoneka, koma ife tanyamula Kuwala. Lolani ife tiwone, phazi ndi phazi, pamene ife tikupita tsopano; mpaka ife tidzakomane, monga “*Ulendo wa Mwendamnjira*, mpaka ife potsiriza tidzagwira pamwamba pa Phiri. Titsogolereni ife, O M’busa. Yehova Wamkulu, titsogolereni ife ndi Mzimu Wanu.”

²¹³ Ndipo ife tikudziwa kuti ife tiri kutali kwa mbambande iyo; koma ife tikuyang’ana kumene ife tinatemedwako, Mbambande yeniyeni, ndipo mwa Iye ife tikudalira. Mungotitengera ife kwa Iye, Ambuye. Perekani ichi, Ambuye.

²¹⁴ Chiritsani anthu onse odwala pano, Ambuye. “Ife tinamuwona Iye wokanthidwa ndi wovutidwa. Koma Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu.” Mbambande ya Mulungu inakanthidwa. “Ndipo Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Chizani odwala, Ambuye, mu Kukhalapo Kwanu Kwauzimu tsopano, pamene ife tikudziwa kuti Inu muli pano.

²¹⁵ Tsukani miyoyo yathu, mitima yathu, ku zoipa zonse, malingaliro onse oipa, kulankhulana koipa konse, zinthu zonse zimene ziri zolakwika. Titsukeni ife. Ndipo ife tikupemphera, Atate, kuti Inu muchize nthenda zathu, ndipo tiroleni ife tichoke pano tikumva kuti ife tiri ana Anu oyeretsedwa. Ndipo ndi Mwazi pa ife, ife tikulankhula kupyolera mu Mwazi, Mawu. Tipatseni izo, Ambuye. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

²¹⁶ Atate Mulungu, pa mipango iyi, idzozeni iyo ndi Kukhalapo Kwanu, Ambuye. Mulole Kukhalapo Kwanu kukhale ndi iyo kulikonse kumene iyo ikupita. Pa chirichonse chimene iyo ikayikidwapo, pa thupi lililonse lodwala, lolani iwo akachiritsidwe. Ndipo chirichonse, ngati pali banja losweka kwinakwake, likonzeni ilo, Ambuye, Wosema wamkulu. Tipatseni izo, Ambuye.

²¹⁷ Tiwumbeni ife, ndipo tipangeni ife ana a amuna ndi aakazi a Mulungu. Ife tikukhulupirira Mkwatibwi akulandira kukonzedwa kwake kotsiriza. Iye adzakanthidwa mu bungwe lathunthu, onse palimodzi, ndiyeno kukolola kwakukulu kudzafika. Mpaka nthawi imeneyo, Ambuye, apangeni iwo a

thanzi ndi okondwa, pokutumikirani inu. Mu Dzina la Yesu. Amen.

Ndimkonda Iye, ndi . . . (Kodi mukumkondadi Iye?)
 Poti Iye anayamba kundikonda
 Nagula chipulumutso changa
 Pa . . .

²¹⁸ Tsopano kodi inu mukumvetsa chifukwa chake ine ndimakudzudzulani inu? Si chifukwa ine ndimakukondani inu . . . osati chifukwa choti ine sindikukondani inu. Ine ndimakukondani inu. Ine ndikufuna Mbambande ya Mbuye. Ine mwina ndikhoza kung'amba ena pang'ono monga chonchi, koma ine ndidzakhala ndi Mbambande, lina la masiku amenewa, ngati ine ndikhalabe bwino pa Mawu awa. Nzolondola.

²¹⁹ Tsopano Yesu anati, “Ichi anthu onse adzadziwa kuti inu ndinu ophunzira Anga, pamene inu mukondana wina ndi mzake.” Ife tiyenera kukhala mu chikondi kwambiri wina ndi mzake!

Nchodala chimango chathu
 Mitima yathu m'chikondi cha Chikhristu;
 Chiyanjano cha mtima umodzi
 Nchonga cha Kumwamba.

Tiyeni titenge manja a wina ndi mzake.

Pamene ife tilekana,
 Zitipatsa kuwawa mkati;
 Koma tidzakhala olumikizidwa m'mtima,
 Kuyembekezera kudzakomananso.

Tenga Dzina la Yesu nawe,
 Mwana wosauka ndi watsoka;
 Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,
 Litenge konse umkako.

Dzina lopambana, O lokoma!
 Chiyembekezo chapadziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba;
 Dzina Lopambana, O lokoma!
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba.

Tsopano kumbukirani, mu ulendo wanu:

Tenga Dzina la Yesu nawe,
 Ngati chishango ku zosamala zonse;
 Pamene mayesero akuzinga inu . . .
 (Mumachita chiani ndiye?) . . . -a,
 Puma Dzina loyera mwa pemphero.

O Dzina Lopambana, O lokoma!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;
Dzina Lopambana, O lokoma!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba.

Mpaka ife tidzaonanenso!

Tiyeni tiweramitse mitu yathu. O, ine ndimakonda kuyimba!

Mpaka tidzaonane pa mapazi a Yesu;
Mpaka tidzaonanenso! mpaka
titadzaonanenso!
Mulungu akhale ndi inu!



MBAMBANDE CHA64-0705
(The Masterpiece)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, Julaye 5, 1964, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1994 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1994 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org